


AHEBRI, MUTU

WACHISANU NDI CHIWIRI ²

 Akudalitseni inu! Ine ndikuganiza, poyamba, ife tiri ndi mwana wamng'ono apa, Doc anandiuza ine pafupi maminiti pang'ono apitawo, m'bale wanga, m'bale mu thupi, yemwe amafuna. . . anali woti adalitsidwe. Ndipo tsopano ngati amayi awo ali ndi ana awo aang'ono omwe akufuna kuti awadalitsire kwa Ambuye, ife tikhala okondwa kukhala nawo iwo pakali pano. Iwo abwere, awabweretse ana awo pano.

²³⁹ Tsopano, ndipo anthu ambiri, iwo, chimene iwo amachitcha, kuwabatiza iwo. Mpingo wa Methodistu umatero, ndipo ine ndikukhulupirira Anazerene. Ine sindiri wotsimikiza. Ayi. Ine ndikuganiza ndi chimene iwo anapatukirana, chinali ubatizo wa ana, Anazereni ndi a Methodistu Yaufulu. Koma, mulimonse, ena a iwo, iwo amachita chinthu china kapena chimzake. Koma, ndipo ena mwa iwo amatsanulira madzi pang'ono pa iwo. Ena amawakonkha iwo. Ndipo, koma ife nthawizonse timayesera kuti tizikhala mwapafupi basi ndi Baibulo momwe ife tikudziwira mwake. Tsopano, palibe Lemba mu Baibulo loti ana azikhala akukonkhedwa, komanso palibe Lemba mu Baibulo loti munthu aliyense azikhala akukonkhedwa. Icho sichinthu cha Mwamalemba. Ilo ndi dongosolo la mpingo wa Katolika.

²⁴⁰ Koma i—koma iwo amatero, amabweretsa. . . Iwo anabweretsa kumene ana aang'ono kwa Yesu. N—ndipo ife ndi oti tizimuimira Iye. Ife tikufuna kuti tizichita chinthu chomwecho chimene Iye ankachita. Iye anaika manja Ake pa iwo n—ndipo anawadalitsa iwo, ndipo anati, “Lolani ana aang'ono kuti abwere kwa ine, ndipo musati muwakanize iwo, pakuti kwa oterewa uli Ufumu wa Kumwamba.” Ndipo ndi chimene ife tikupitiriza kuchita pano pa kachisi, pamene ife tikuyesera kuti tipitirize nalo Baibulo lenileni, njira yopatulika, mwakukhoza momwe ife tikudziwira.

²⁴¹ Chotero tsopano, ngati amayi awo, kapena amayi aliwonse omwe ali ndi ana awo oti adalitsidwe, pamene Mlongo Gertie akuimba *Abweretseni Iwo Umo*, bwanji, inu muziwabweretsa iwo ku guwa. M'bale ndi ine tibwera pansipo ndi kudzawadalitsira ang'ono awo kwa Ambuye. Chabwino.

M'bale Neville. [M'bale Branham ndi M'bale Neville akudalitsa ana. Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

²⁴² Zikomo inu, Mlongo Gertie. Izo nzabwino kwambiri. Ndi angati amawakonda ana aang'ono? Ngati inu simutero, pali chinachake cholakwika ndi inu, pali chinachake cholakwika.

²⁴³ Tsopano, usikuuno, tsopano kuti tipite mu utumiki wina wonse. Ife . . . chifukwa chimene ine ndabwerera kuno usikuuno. Kawirikawiri pa masiku awa pamene ife tiri ndi misonkhano ya machiritso, ine ndimangokhala nawo pafupi umodzi pa tsiku, chifukwa izo zimandipatsa ine kugwedeza koteroko. Inu simumadziwa konse izo. Ndipo kuno kwathu zimakhala zoipa pawiri monga kwina kulikonse.

²⁴⁴ Ndipo ine ndinali kupepesa pa kupanga kulakwitsa koteroko monga ine ndinachitira ndi izo mmawawu. Koma chinthu choyamba chimene chinandisokoneza ine, chinali pamene Billy anabwera kudzandiuza ine kuti iye sanakhoze kuwapeza anthu okwanira kuti awapatse makadi a pemphero. Iye anangokhoza kupereka pafupi khumi ndi awiri kapena khumi ndi anai. Ndipo iye anali . . . Panalibe aliyense yemwe amafuna makadi a pemphero. Ine ndimalingalira chirichonse chinali bwino bwino. Kotero ndiye, ndi zimenezo, ine sindinaganize konse . . . Ndiyeno pamene ine ndinayamba kuitana makadi a pemphero awo, ine ndimaganiza kuti nditenga onse khumi kapena khumi ndi awiri, kapena aliwonse omwe analipo mkati muno. Ndinawaitanira iwo pano. Ine ndinafika ku nambala inayake, chinachake, ndipo iyo siimaitanika. Ndipo ine ndinaitana. Iyo siimayankhidwa. Ndipo ine sindinaganize konse za iyo mpaka Akazi a Woods atandiitana ine. Iwo anati, “M’bale Branham, Billy amatenga makadi amenewo ndipo amawasakaniza iwo palimodzi, ndipo amangowapereka iwo. Iye mwina anali ndi nambala firii iyo,” (sichoncho izo?) “nambala firii mu thumba lake.”

²⁴⁵ Zedi, iye kawirikawiri amapereka makumi asanu onse. Pamene iye awabweretsa iwo kwa anthu, iye amangowasakaniza iwo. Kutali aliyense . . . Izo sizokuti nkunena, “Ndipatse ine nambala wani.” Kapena, ife mwina sityambira pa nambala wani. Ife tikhoza kuyambira pa fifite, inu simukudziwa, ndi kumabwera chammbuyo. Ife mwina tikhoza kuyambira pa eyiti ndi kumapitirira nazo. Tikhoza kuyambira pa twente ndi kumapitirira nazo. Ife sitimadziwa. Koma iye amangowasakaniza iwo ndi kuwapereka iwo kwa anthu pamene iwo amawafuna iwo. Ndipo mosaganizira mmawa uno, ine mwina ndinaitana foro kapena faifi ena, ndipo iwo mwina munalibe mmenemo, chifukwa iwo mwina akhoza kukhala kuti anali mmatwente kapena mmasate penapake, inu mukuona. Ndipo, ndiye, koma Ambuye anazikonza izo, koma basi izo ziribe—kupanikiza kwenikweni kwa izo, monga izo zimachitira kutali ndi kwathu kuno. Ine mwina sindidzayesera izo—kuyesera izo kachiwiri.

²⁴⁶ Koma, kuno osati kale litali, ine ndinawafunsa Ambuye ngati Iye akanatipatsa ife msonkhano wabwino, umene ine ndinalonjeza kuti i—ine sindikanati ndiwafunse Iwo izo kenanso, chifukwa icho chakhala chiri chinthu chovuta chotero. Ndipo izo ndi zosiyana ndi Malemba. Mukuona? Ndipo ngati inu . . .

Icho ndi chomwe chimapangitsa izo kuvuta pa ine. Chifukwa, podziwa izo, izo zimandipatsa ine—kugonjetsedwa, pa kuyamba pomwe. Mukuona? Ine ndine wogonjetsedwa, pa kuyamba pomwe.

²⁴⁷ Komabe, winawake anamuitana winawake madzulo ano. Akazi a Woods anaitanidwa ndi winawake. Ndipo ananena, kuti, “Winawake mu mpingo anaitanidwa mmawa uno, pa zokhudza mwamuna yemwe anali atadwala kwambiri, mbiri, yemwe anabwera kwa Khristu madzulo ano, pambuyo pake.” Kuti—munthu yemwe anali atadwala kwambiri wabwera kwa Khristu.

²⁴⁸ Ndipo chinthu china, Akazi a Woods anandiuza ine kuti ine ndinayankhula kwa mlongo wawo, mlongo wachikulire, yemwe ine ndinakhala kwenikweni mu nyumba yake tsiku lina ndi kudya nkhumaliro ndi iye, kapena mgonero ndi iye, uko ku Kentucky. Ndipo Mulungu Wamphamvuzonse akudziwa kuti ine sindinamuzindikire mkazi ameneyo. Mukuona? Ndiko kulondola. Basi... Masomphenya ndi ochita mwawokha. Ife sitimadziwa konse momwe iwo ati ayendere kapena chomwe chiti chichitike. Izo zimakhala kwa Mulungu, ndi z—zomwe zingati zichitike. Koma ine ndimadziwa, pakuwadikirira iwo, kudikirira pamene.

²⁴⁹ Ndipo tsiku lina pamene msungwana wamng’ono uyu anali kuno, yemwe amayenera kuti akhale ndi kuzindikira, chomwe ine, osati... Mukuona, ngati Mulungu angapereke icho kwa dziko lonse, icho chingakhale chabwino; koma ngati izo zitatero, izo zingakhale zosiyana kwa zomwe Iye anandiuza ine kutsidya kwa msewu kuno, inu mukuona, zaka zingapo zapitazo. Ndipo ife tinkafuna kuti tikhale otsimikiza kuti izo zinali zolondola, ndi kuwulola mpingo, pokhala kuti iwo unali kuno, uziwone izo. Ndipo kotero ine ndinawaimbira izo Akazi a Snyder. Mlango Snyder. Iwo ali pano penapake. Iye ali pang’ono pokha ndi vuto lakumva. Ndipo dona wamng’ono ankayankhula izo motsika, ndipo anati, “Inu muli ndi vuto la misempha,” kapena nyamakazi, chinachake chonga izo.

²⁵⁰ Chimene, ine ndinkadziwa kuti munali mchiuno mosweka. Ndipo kotero... Ndiyeno Mzimu Woyera unazibweretsa izo umo mmawawu. Mukuona?

²⁵¹ Tsopano, chomwe izo ziri, izo ndi mphatso Yauzimu, ndipo iyo imagwira ntchito mwayokha. Koma chomwe chimapangitsa izo kuvuta kwambiri kuno mu mzindawu, moona, i—ine ndimadzimangiriza, nthawizonse, pa kuwapempherera odwala kuno. K—kapena... ine ndimapita, kuwauza anthu izi. Ine ndimapita, nkuti, “Tsopano Ambuye akupangitsani inu kuchira. Yesu anakuchizani inu pamene Iye anakuferani inu, zaka naintini handiredi zapitazo. Apo pomwe inu munachiritsidwa. Tsopano, kunena momwe ziriri ndi Mulungu, kunena za momwe

ziriri kwa Khristu, inu munachiritsidwa, zaka naintini handiredi zapitazo. Matenda anu anapita. Izo zitengera chikhulupiriro chanu kuti chichite izo.

²⁵² Ndiyeno munthu ameneyo akhoza kumapita pozungulira ndi kusapeza bwino. Ndiye munthuyo amabwera apo, nkuti, “M”bale Branham anandiuza ine kuti ndinali bwino.” Mukuona? Ine ndikukuuzani inu zomwe Mulungu ananena.

²⁵³ Tsopano, pamene izo ziyankhulidwa molunjika kwa munthuyo, molunjika, “Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE,” pa chinthu chinachake chomwe chiti chichitike. Izo zingatsimikizire kwa inu apo pomwe kuti machiritso anu apezedwa kale. Chikhulupiriro chanu chawasindikiza iwo. Mukuona? Lonjezo ndi lanu. Iwo si mawu anga. Awo ndi Mawu a Mulungu, kuti inu mwachizidwa kale. Mukuona? Koma inu basi... Mwanjira ina imzake, i—ine sindimakhoza basi kuzifikitsa izo poti zilowerere mkati, kwa akwathu kuno mu Jeffersonville. I—ine sindimakhoza basi kuzifikitsa izo poti zichitike. Ine ndikudziwa. Ine ndimayesera kuti ndizifotokoze izo mwabwino basi monga ine ndingathere, ndipo izo basi—izo sizimachitika basi. Ndizo zonse. Ine ndikati . . .

²⁵⁴ Kuno, osati kale litali, ine ndinapita ku banja, kwa bambo, ndipo bamboyo anali akufa. Ndipo iwo anandiitana ine, “Bwerani, mudzamupempherere iye. Adokotala akuti iye sakhala moyo kufikira mmawa.”

²⁵⁵ Ine ndinalowa umo. Ndipo mnyamatayo anati kwa ine, “Bambo Branham, ine sindikufuna kuti ndife.” Bwanji, ndithudi mnyamatayo samafuna. Iye anali ndi banja la ana awiri kumeneko.

²⁵⁶ Chabwino, ine ndinakafika uko. Ine ndinati, “Tsopano, taona, dokotala wako ndi ndani?” Iye anandiuza ine. Ine ndinati, “Tsopano, adokotala akhoza kuti anati iwe unali, iwe ukanati ufe, koma Mulungu sananene panobe kuti iwe ufa.” Ine ndinati, “Tsopano, malingana ndi Baibulo, iwe unachiritsidwa kale, chifukwa Yesu anafera machiritso ako.”

²⁵⁷ Iye anati, “Kodi inu mukukhulupirira kuti ine ndikhala bwino?”

²⁵⁸ Ine ndinati, “Ine mwamtheradi ndikukhulupirira izo.”

²⁵⁹ Chabwino, ngati ine ndikanapita kukamupempherera munthu, ndi kusagwiritsa ntchito mtundu wa chikhulupiriro umenewo, kuti ndikhulupirire mmalo mwa iye; ngati ine ndingati, “O, ayi, ayi, ngati adokotala anena kuti inu mufa, inu mupita kukafa. Izo zakhazikitsa icho tsopano.” Tsopano, kodi uyo sakanakhala munthu wina woti abwere adzamupempherere wodwala? Ine sindikanamufuna munthu ameneyo mu nyumba yanga, kuti andipempherere ine. Ine ndimafuna winawake yemwe, ngakhale ngati iye sanaziwone izo, kapena ayi, iye

akanatenga chikhulupiro ndi kuima pa lonjezo mmalo mwanga. Ndiko kulondola. Ndipo ine ndinati. . . iye. . .

260 Iye tinapita ndipo tinali ndi pemphero. Ine ndinati, “Tsopano khalani wolimba mtima bwino.”

261 Iye anati, “Kodi inu mukutanthauza kuti ine ndikhala bwino?”

262 Ine ndinati, “Bwanji, zedi. Mawu a Mulungu anati iwe ukhala bwino. Mukuona, ‘Ngati iwe ungati ukhulupirire, zinthu zonse ndi zotheka.’”

263 Iye anati, “Chabwino, ine ndikhulupirira Izo.” Ndipo anapita kunjani ndi kukanena kwa mkazi wake, izo.

264 “Munthuyu akufa, si choncho izo?”

265 “Inde, iye akufa.” Ndipo chotero tsiku lotsatira, bamboyo anafa, kapena masiku angapo zitachitika zimenezo.

266 Ndiye mkazi uyu anapita ndi kukayamba kumwa ndi kumapitirira nazo. Ndipo mmodzi wa madikoni, ine ndikukhulupirira iye anali, wa mpingo uno, anapita kwa mkaziyo ndipo anakamufunsa iye ngati iye akanati abwerere ndi kubwerera ku mpingo. Iye anati, “Ine sindingati ndimukhulupirire wina aliyense. Mlaliki Branham kubwera kuno ndi kumupempherera mwamuna wanga, anati iye akhala moyo, ndipo iye anafa mu masiku awiri kapena atatu otsatira.” Anati, “Ine sindingati ndimukhulupirire.” Tsopano *iye* ali nkufa. Chabwino.

267 Koma, mulimonsebe, inu mukuona, izo zikungosonyeza kuti anthu samapereka chidwi ku zomwe iwe ukunena. Mukuona? Ndithudi. Ngati ine nditamupempherera munthu, ndipo i—ine nkuwauza anthu amenewo kuti iwo kuti akhala moyo. Ine ndikukhulupirira kuti iwo akhala moyo. Koma, ziribe kanthu, ngati mawu anga akanakhala mwamtheradi PAKUTI ATERO AMBUYE, ndipo inu nkusawakhulupirira Iwo, inu mukanafa, mulimonse. Ndithudi. *Apa* pali PAKUTI ATERO AMBUYE, ndipo ambiri a iwo amamulandira Iye ndipo amafa. Ambiri a iwo amapita ku gehena, pamene, PAKUTI ATERO AMBUYE, “Inu simumayenera kutero.” Ndi kulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Zedi. Mukuona? Ndi zomwe. . . Izo zonse zimakhazikika pa chikhulupiro chanu.

268 M’bale Collins, ine sindikuganiza kuti iye ali muno usikuuno. Koma pomumvetsera iye mmawa uno, iye anapereka kuyankhula kwamphamvu kwambiri pa izo. Mukuona? Mukuona? Iye anatero. Iye anati, “Tsopano, chikhulupiro chomwecho chimene inu muli nacho kunochi, inu muyenera kuti muzikakhala nacho kunjani uko. Chifukwa, ndi chikhulupiro chanu chanu, osati mu chipembedzo chanu, koma mwa Khristu. Inu muyenera kumakakhala nacho chikhulupiro chimenecho.” Ndizo basi ndendende kulondola. Mwamtheradi.

²⁶⁹ Ndipo machiritso Auzimu amakhazikika pa chikhulupiriro chanu. Koma molingana ndi Mawu a Mulungu, PAKUTI ATERO AMBUYE, kuti munthu aliyense anachizidwa pamene Yesu anafa pa Kalvare, “Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, ndi mikwingwirima Yake ife *tina* chiritsidwa.” Nkulondola uko? Ife *tina*. Baibulo linati, “Inu munachiritsidwa.” Chotero musamapeze cholakwika ndi ine, ine ndangokhala mlaliki wa Mawu. Inu mupite mukamuze Mulungu kuti Iye anatiuza chinachake cholakwika, ndipo Mulungu akakuuzani inu pomwe pali kufooka kwanu ndiye. Mukuona? Chotero, ndi chikhulupiriro chanu. Yesu anati, “Ngati inu mungati mukhulupirire. Ngati inu mungati mukhulupirire.”

²⁷⁰ Tsopano, pamene inu mumva Mzimu Woyera kuti watsimikizira chikhulupiriro chanu ndipo wachilimbikitsira icho pansu, ndi kuti, “PAKUTI ATERO AMBUYE, ‘Mawa pa nthawi *ino*, iwe udzakhala ndi chinthu *chinachake*. Chinthu *chinachake* chidzachitika. Ichu chidzakhala cha kuno mwanjira *inayake*, ndipo inu mudzakomana ndi chinthu *chinachake* kuno. Ichu chidzakhala chizindikiro kwa inu.’” Tsopano, inu muchiyang’anire icho. Iyo ndi ntchito yotsirizidwa, apa pomwe tsopano.

²⁷¹ Koma pamene izo zibwera ponena za machiritso Auzimu, ine ndimayenera kuti ndiziyika machiritso Auzimu pa maziko omwewo, a chikhalidwe chimenecho, monga chipulumutso. Wina aliyense wa inu, ziribe kanthu zomwe inu munachita, inu munapulumutsidwa kale kuchokera pamene Yesu anafa, chifukwa Iye anafa kuti adzachotse machimo a mdziko. Koma izo sizidzakuchitirani inu ubwino uliwonse mpaka inu mwanokha mutachilandira icho ndipo icho nkukuchitikirani. Koma kunena za machimo anu, iwo anakhulukidwa kale. Ndiko kulondola. Iye... “Taonani Mwanawankhosa wa Mulungu amene achotsa machimo a mdziko.” Mukuona? Ndi inu apo. Tsopano muzikumbukira zimenezo.

²⁷² Tsopano, ine ndikudziwa kuti mu kuphunzitsa, mu Malemba, ndife gulu losakanizikana. Ndipo nthawi zambiri, mu Bukhu ili la Ahebri, lomwe liri maka Bukhu lakuya. . . Ine ndiyenera kuti ndilisiye ilo kwa kanthawi tsopano. Ine ndiyesera usikuuno kuti nditsirize gawo lotsiriza la mutu wa 7 uwo.

²⁷³ Ndipo tsopano pali mafunso ambiri mu malingaliro mwanu, mopanda kukaika. Ambiri a inu muli ndi mafunso, ndipo ine ndikanakhala nao, nanenso. Tsopano, nthawi yotsatira, Ambuye akalola, pamene ine ndidzabwere muno. . .

²⁷⁴ Ine ndikupita ku Michigan tsopano. Ndiyeno, kuchokera ku Michigan, ine ndidzapita ku Colorado. Ndipo kuchokera ku Colorado, kupita ku Chigwa Chakumadzulo. Tsopano—tsopano, pamene ife tidzabwera muno, Ambuye akalola. . . Tsopano, ine sindikudziwa. Ngati ine sindikakhala ndiri ku

Chicago, Lamlungu, ine mwina ndingadzakhale nditabwerera kuno kwa usiku wa Lamlungu likubwerali.

275 Tsopano ife tikuwagwira abusa athu kunja kwa guwali kwa pafupi masabata asanu ndi limodzi, monse kudutsa i—i—izi, bukhu ili pano. Mukuona? Tsopano ife. . . Ine sindimakonda kuchita zimenezo. M'bale Neville ndi wokonedwa, wokoma, m'bale wachifundo. Ndipo ine ndikutsimikiza kuti mpingo uno umamukonda M'bale Neville.

276 Mwa njira yomweyi, pamene ine ndikuyankhula; winawake, kuzungulira kumudzi kuno kwina wake, ndi wolakwa pakulemba makadi ena, kuti amuchotse M'bale Neville pa guwa lino. Inu muyenera kuti muzikhazikitse zimenezo ndi ine. U-nhu. Ndiko kulondola. U-nhu. Inde, ndithudi. Tsopano, ine ndikufuna inu. . . Anati dik-. . . chinachake chokhudza gulu la madikoni. Gulu la madikoni liribe chinthu chimodzi chochita ndi m'busa ameneyo. Ayi, bwana. Osonkhana, mwathunthu, ali nawo ulamuliro wonse. Si. . . Gulu la madikoni angokhala amuna apolisi pano mu mpingo uno, kuti azingosungitsa bata ndi zina zotero. Koma pamene zibwera pa malamulo, mpingo wonse umayenera kuti unene chomwecho. Mpingo uno unamangidwa pa kuchita kwawokha kwa mpingo uli wonse. Chotero, ine ndiribe kanthu koti ndinganene za kumuchotsa m'busa uyu, kapena kuyikamo wina. Ine nyumbayi ndi yanga; iyo inaperekedwa kwa mpingo. Inu nonse ndinu mpingo. Inu anthu ndi omwe mumalamulira. Inu ndiye mpingo, inueni. Ndipo Mpingo, Mpingo woyera wa Mulungu ndi wochita mwawokha, mwa Mzimu Woyera mu Mpingo umenewo. Ndipo chinthu chokha chimene ine ndachita ndi kukhala mwini wa nyumbayi, kuipereka iyo kwa mpingo uwu, monga kuipereka iyo kuti ikhale tchalitchi, ndipo izo ndi zosaperekera msonkho. Ndipo mpingo umasankha abusa ake ake. Ine ndiribe kanthu kochita ndi izo. Ndipo njira yokha yomwe abusa awa akanati achokere konse, akanakhala ali abusa kulingalira kusankha okha kuti achoke, kapena kuchuluka kwa mavoti a mpingo akanati anene, "Tisinthe m'busa." Ndiye njira yokha. Palibe gulu la madikoni lingathe kuchita zimenezo. Gulu la madikoni limangosungitsa bata ndi zinthu mu mpingo.

277 Matrastii, iwo alibe kanthu kochita ndi izo, amangokonzetsa tchalitchi. Ndipo iwo sangathe kuchita izo mpaka patakhalala. . . Gulu lonse la matrastii likakomana ndi kuti, "Ife timanga *ichi*, kapena ife tichita *icho*." Ndiye iwo amayenera kuti amufunse msungichuma ngati iwo ali nazo ndalama zochitira izo. Inde, bwana.

278 Koma ngati pali dandaulo lirilonse lotsutsa membala aliyense, ngati membala ali ndi chidandaulo pa wina ndi mzake, kapena chinachake chitavuta, inu muyenera kuti mupite kwa m'bale ameneyo, inumwini; ndi kukayankhula naye iye, inu ndi iyeyo nokha. Ndiye ngati iwo sati azilandire izo,

ndiye chinthu chotsatira chomwe chingachitike, inu mumutenge mmodzi wa madikoni kapena winawake, ndipo apite ndi inu kwa m'bale ameneyo. Ndiye ngati iye sakakulandirani inu, ndiye inu mubwere mudzanene izo kwa mpingo. Ndiye ngati mpingo. . . Ndiye ngati iye saulandira mpingowo, ndiye Baibulo linati, "Muwasiye iwo akhale ngati achikunja ndi awamba." Ndiko kulondola.

²⁷⁹ Ndipo munthu aliyense yemwe akumudziwa munthu wolakwa, ndipo inu nkusapita kwa iwo ndi kukayankhula, ndiye ndinu gawo la mpingo wa Mulungu lomwe liti lidzakayankhire kwa tchimo limenelo. Ndiko kulondola.

²⁸⁰ Ndipo ngati munthu aliyense ndiye ali nacho—chidandaulo motsutsa dikoni, kapena motsutsa dikoni kapena winawake mu mpingo, izo zimatengera anthu atatu. Anthu atatu azibwera ndi kuti, mboni, pakamwa pa mboni ziwiri kapena zitatatu. Kubwera kudzawauza abusa kuti pali chidandaulo motsutsa dikoniyo. Ndiye ngati pali chidandaulo motsutsa dikoni, dikoni si—munthu wolungama, m—munthu wangwiro. Iye ayenera kumagwira udindo wa dikoni, mopanda chomunenera, ndiyeno azipezeka wopanda chomunenera. Ndipo ngati gulu limenelo lipeza kuti dikoni ameneyo sakugwira udindo umenewo, iye amatenga atatu limodzi naye ndipo amazitengera izo kwa abusa. Dikoni ameneyo amafunsidwa kuti akhale kunyumba usiku umenewo. Ndiyeno abusa kuchokera. . . amabwera ndi kuwabweretsa osonkhana onse palimodzi, napereka chidandaulocho. Ndipo ngati osonkhana avotera kuti dikoniyo azipitirira, dikoniyo amapitirira nawo. Ngati iye am- . . . avotera kuti dikoniyo achotsedwe, iwo asankhe dikoni watsopano usiku womwewo. Mukuona?

²⁸¹ Chotero, palibe munthu mmodzi ali ndi kanthu kochita mu izi. Ndi kuchuluka kwa anthu. Inde, bwana. Ngati twente amuvotera iye, ndipo twente wani avotera momutsutsa iye, iye amachoka; kapena, mosinthanitsa. Mukuona? Izo ziri, ndi kuchita kwawokha kwa mpingo uliwonse ndipo, ndiye, aliyense wa mamembala amakhala nacho chonena mu mpingo. Chirichonse chikachitika, molakwika, ndiye iwo akhoza kubwera apo pomwe, ndipo chinthu chokha chomwe iwo ayenera kumachita ndi kumakhala pamaso pa Mulungu kuti iwo mwamtheradi akuwona kuti palibe kanthu kakutchinga kayendetsedwe ka mpingo.

²⁸² Koma ulamuliro wathunthu ndi wamphumphu wa mpingo ndi m'busa. Kawerengeni zimenezo mu Baibulo, mukawone ngati ilo si dongosolo la Baibulo. Ndizo ndendende kulondola. Palibe wina ali pamwamba pa mkulu. Ine ndiribe kanthu kochita ndi zomwe M'bale Neville amachita pano. Izo ziri kwa inu ndi M'bale Neville. Ngati M'bale Neville angafune kuti azilalikira Chiphunzitso cha Mboni za Yehova, izo ziri kwa iye ndi inu. Mukuona? Ngati iye akufuna kuti azilalikira

chirichonse chimene iye akuchifuna, izo ziri pakati pa inu ndi iye. Ndizo zonse. Ngati osonkhana amuvotera iye mmenemo, kuti azilalikira zimenezo, izo ziri bwino bwino. Izo ziri kwa iye.

²⁸³ Chinthu chokha chimene ine ndikuchita, ndi kungokhala mwini wa malowa. Ndipo ngati chinthu china chimzake chibwerapo, zomwe ziri monga kumuchotsa m’busa, ndipo iwo akufuna kuti atenge voti pa zimenezo, inu simungamufunse dikoni kuti achite zimenezo. Inu mukanabwera kudzandifunsa ine. Ine ndikanabwera, nkuti, “Ngati inu mukufuna kuti mumuchotse m’busa, ndiuzeni ine chifukwa chake. Kodi iye wachita chirichonse?”

²⁸⁴ “Inde. Ife tinamugwira iye, ataledzera. Kapena, ife tinamugwira iye akuchita *izi*, kapena amachita chinachake chomwe sichinali choyenera.”

²⁸⁵ “Kodi inu muli nazo mboni zitatu pa izo?”

²⁸⁶ “Inde. Ife tiri nazo.”

²⁸⁷ Mboni zimenezo ziyenera kuti poyamba ziziyesedwa. “Musati muzilandira chonenera motsutsa mkulu kupatula ziri mwa mboni ziwiri kapena zitatu, ndipo muzilola izo poyamba zizitsimikiziridwa; motsutsa mkuluyo.” Ndiye inu muyenera kuti muzilumbirira kwa izo, kuti inu munaziwona izo; ndi kutsimikizira izo, kuti inu munaziwona izo.

²⁸⁸ Ndiyeno, ngati inu munatero, ndiyeno tchimo limenelo lizidzudzulidwa poyera, kuti, “Ndi cholakwika.” Ndiye nkuti, “Osonkhana, kodi inu mukufuna kuti musinthe m’busa wanu?”

²⁸⁹ Ndipo ngati osonkhana avotera, “Mukhululukireni iye, ndipo musiyeni iye azipitirira panobe,” ndi momwe izo ziyenera kuimira. Mukuona? Izo, kodi izo si zachilungamo mokwanira momwe mungamayendetsere mpingo? Ndizo zomwe Baibulo linanena. Ife tiribe mabishopu ndi oyang’anira, ndi magulu ndi zina zotero, zomuchotsa *uyu* ndi kukhala nao ulamuliro wochuluka. Palibe wina yemwe ali ndi ulamuliro pano koma Mzimu Woyera. Ndiko kulondola. Iye amachititsa kuchotsako. Ndipo ife timamutenga Iye ngati kuchuluka kwa anthu, njira yomwe anthu apita.

²⁹⁰ Ndiyeno ngati mbali imodzi ikufuna kuti achite *ichi*, ndipo mbali inayo akufuna kuti achite *icho*, ndipo mbaliyo nkupambana. Mbali yolephera, kodi iwo achita nazo chiani izo? Alumikizane limodzi nawo ena onsewo, ndi kuti, “Ife tinali kulakwitsa, ndiye. Ife tizipitirira nazobe, chifukwa Mzimu Woyera wapanga kusankha kumeneko.” Mukuona? Ndizo ndendende kulondola.

²⁹¹ Monga ma Democrat ndi ma Republican, utali wonse womwe ife tikuima ngati demokarase, monga Achimereka. Ngati ma Democrat akulamulira, ma Republican azikankhira apo pomwe limodzi nawo; ma Republican akamalamulira, ma Democrat

azikankha mopitirira. Mukuona? Ndizo ndendende basi zomwe zimati panganga ife kukhala fuko. Pamene ife tiswa izo, ife timaswa demokarase yathu. Ndiko kulondola. Ma democrat akati, “Ine sindimachita kanthu; ma Republican ndiwo alimo.” Ndiye ife tigwa. Ndine wachi Kentucky: limodzi ife timaima, ndipo tikagawanikana ife timagwa.

²⁹² Tsopano, ngati pali chirichonse cholakwika mu mpingo chomwe inu mukuchidziwa konse, winawake payekha kapena munthu wina kapena chirichonse, inu muli okakamizikira pa ntchitoyo ndipo mudzakayankha pamaso pa Mulungu ngati inu simuchikonza chinthu chimenecho chithe; inu, mpingo. Tsopano, kumbukirani, izo siziri pa mapewa anga. Izo ziri pa anu. Ndipo chirichonse cholakwika mu mpingo, Mulungu adzakupangani inu kuyankhira pa icho. Ndiko kulondola. Umo ndi momwe Iye amayendetsera mpingo wake. Umo ndi momwe izo ziriri mu Baibulo. Ndilo dongosolo la Baibulo. Ndiko kuchita mwawokha kwa mpingo uliwonse. M’busa ndiye mutu. Ndiko kulondola. Amen.

²⁹³ Tsopano, kubwera ku Uthenga wodala, wakale uwu kuno. Inu, tsopano ine ndikufuna inu kuti mudziwe izo. Izi zikujambulidwa pa tepi, kumbukirani, Uthenga uwu. Ndipo zojambulidwa pa tepi za mpingo, dongosolo ndi malangizo a mpingo, ziri pa zojambulidwa pa tepi. Izo ndi molingana ndi Baibulo. Ife sitimayendetsa izo; palibe wina yemwe ali patogolo. Ayi. Tonse, ndife tonse ofanana. Koma, ife tiri naye mtsoholeri, uyo ndiye m’busa, utali wonse pamene iye akutsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Zoon. Chabwino.

²⁹⁴ Tsopano, muno, pakhala pali mafunso ambiri. Chotero nthawi yotsatira yomwe iwo ati adzaipereke. . . Ndipo M’bale Neville adzaziika pa wailesi kuti ine ndidzakhala ndiri kuno, inu mudzalembe apo funso lanu, chotero kuti inu ndi ine tikhoza kukangana pa izo limodzi. Mutero inu? Chabwino.

²⁹⁵ Ine ndikudziwa ine ndaphunzitsa pa kupirira kwa oyer. Ine ndaphunzitsa pa Umulungu wapamwamba wa Yesu. Ine ndaphunzitsa pa chitetezero cha wokhulupirira, ndi kudzedweratu, kukonzedweratu, ndi zambiri za zinthu zimenezo. Zomwe, ine ndikudziwa, mwa osonkhana anga muli ambiri amwalamulo, zomwe ziri bwino bwino mwangwiro. Mwamtheradi. Koma, tsopano, zinthu, ine ndine wamwalamulo, nanenso, ndipo ine ndine wa Chikalvini. Ine ndimangolikhulupirira Baibulo. Ndizo zonse.

²⁹⁶ Tsopano, ngati ena a mafunso, amenewo. Ndipo ine ndaphunzitsa pa maumboni, zomverera, ndi zina zotero, ndi zinthu zina zonse izo zomwe inu mukhoza kusagwirizana nazo. Chotero limodzi la mausiku awa, mwinamwake. . . Tiyeni tilipange ilo. . .

Kodi inu muli changu chachikulu kuti mubwererenso pano? [M'bale Neville akuti, "Ayi."—Mkonzi.]

Tiyeni tilipange ilo Lachitatu usiku, Lachitatu likudzali usiku, ndiye i—ine ndikuganiza i—ine ndikhoza kudzakhala nazo izo ndiye. Kabweretseni funso lanu Lachitatu usiku, dzaliyikeni ilo pano pa nsanja, ndipo funso lokhudza Baibulo, chabwino, la zomwe ine ndakhala ndikuziphunzitsa tsopano. Ndipo Lachitatu usiku. Ndiyeno pofika Lamlungu lotsatira, ndiye, ine ndikuganiza i—ine ndiyenera kuti ndidzakakhale ndiri mu Chicago, mulimonse. Ndipo ine ndizidzapita kuchokera kumeneko ku Michigan. Ambuye akalola, ine ndidzakhala ndiri kuno Lachitatu usiku, kuti ndidzayesere kuyankha funso mopambana momwe ine ndingathere. Ndipo tsopano Ambuye akhale achifundo kwambiri.

Tsopano tiyeni tiweramitse mutu wathu, mphindi yokha.

²⁹⁷ Tsopano, Ambuye wodala, ichi ndi chuma Chanu chachikulu. Iwo ndi mpingo Wanu. Ndi Inuyo, Ambuye, yemwe mukusuntha, ndipo ife tikufuna kuti tizisuntha pamene Mzimu wa Mulungu ukutisuntha ife. Ndipo ife tikupemphera tsopano kuti Inu mutidalitse ife. Ndipo pamene ife tikubwereza Uthenga uwu, ndi kufika mu zinthu zakuya izi, ife tikupemphera kuti Mzimu Woyera uwululire izo kwa ife momwe ife tiriri ndi chosowa. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake. Ameni.

²⁹⁸ Tsopano, o, ine . . . Bukhu ili la Ahebri, ine ndimaliwerengera ngati limodzi la Mabuku aakulu.

²⁹⁹ Kenako popitirira pang'ono, izo zikhoza kukhala kuti i—ine ndiri . . . ndikupita kutsidya kwa nyanja, chimene icho, ngati Mulungu aloleza, ine ndikhala ndikuchita posakhalitsa ndithu. Ine ndiyenera kuti ndipite ku Afrika molingana ndi masomphenya. Ine ndikuganiza ine sindidzachita bwino mochuluka mu misonkhano yanga mpaka ine nditapita ku Afrika ndi kukakwaniritsa masomphenya amenewo. Tsopano, ndiye, iyo idzakhala mwinamwake nthawiina yophukira ikudzayi.

³⁰⁰ Koma pakati pa nthawi imeneyo, ine ndikanakonda kuti ndidzatenge bukhu limodzi lina kuchokera mu Bukhu la Ahebri, ilo ndi, mutu wa 11 wa Ahebri. Ndi kudzakhala pafupi sabata mu mutu wa 11 uwo, ndi kudzatenga limodzi lirilonse la makhalidwe amenewo kapena chikhalidwe, ndi kutulutsamo makhalidwe awo. Mukuona? "Mwa chikhulupiriro, Nowa," ndiye nkutenga moyo wa Nowa. "Mwa chikhulupiriro, Abrahamu," ndiye nkutenga moyo wa Abrahamu. "Mwa chikhulupiriro, Abele," ndiye nkutenga moyo wa Abele. Mukuona? Ndi kuzibweretsa izo mmusi. Kodi inu mungadzakonde izo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] O, izo zingadzakhale, ife tidzatenga Baibulo lonse apo ndiye. Ndiyeno ife tidzayesera izo, mwinamwake, mulimonse, titi, sabata kapena masiku khumi a misonkhano,

msonkhano umodzi basi pambuyo pa umzake, mu chitsitsimutso monga, nthawiina kudutsa cha mu tchuthi cha Khristimasi, kapena chinachake chonga izo, Ambuye akalola.

³⁰¹ Tsopano, mu mutu wa 7 wa Bukhu la Ahebri, ife tinakomana nalo khalidwe lalikulu ili. Ndani angandiuze ine lomwe linali dzina Lake? [Osonkhana akuti, “Melkizedeki.”—Mkonzi.] Melkizedeki. Tsopano, kodi anali ndani Melkizedeki uyu? Iye anali wansembe wa Mulungu Wammwambamwamba. Iye anali Mfumu ya Salemu, chomwe anali Mfumu ya Yerusalemu. Iye analibe abambo aliwonse, kapena iye analibe amake aliwonse. Iye analibe nthawi yomwe Iye anabadwa konse, kapena Iye sadzakhala konse ndi nthawi yomwe Iye ati adzafe. Tsopano, ife tikupeza kuti uyo ayenera kukhala ali Wamuyaya.

³⁰² Ife tinapeza kuti mawu oti *kwanthawizonse* amatanthauza “danga la nthawi.” Kodi inu mukukumbukirabe izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Danga la nthawi, ndilo kwa nthawizonse ndi kwanthawizonse. Ndipo *kwanthawizonse* ali kuchitiridwa umboni, nthawi zambiri, mu Baibulo ngati “d—danga la nthawi.”

³⁰³ Koma, Umuyaya, ndipo pali mtundu umodzi wokha wa Moyo Wamuyaya, ife tinapeza izo. Ndi kulondola uko? Mulungu ali nawo Moyo Wamuyaya umenewo, yekha. Ndi kulondola uko? Mtundu umodzi wokha wa Moyo Wamuyaya. Palibe mawu otero monga “chilango Chamuyaya.” Chifukwa, ngati iwe uli woti udzakalangidwe kwa Umuyaya, iwe uyenera kukhala uli nawo Moyo Wamuyaya. Kutu udzakalangidwe Mwamuyaya, iwe udzasowa kudzakhala nawo Wamuyaya. Ndipo ngati iwe uli nawo Moyo Wamuyaya, iwe sungati ukhale ukulandidwa, mukuona, ngati iwe uli nawo Wamuyaya. “Iye amene amva Mawu anga, nakhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha.” Ndi kulondola uko? Moyo Wamuyaya, chifukwa inu mukhulupirira. Chabwino, ngati inu muli nawo Moyo Wamuyaya, inu simungakhoze kulandidwa, chifukwa inu muli nawo Moyo *Wamuyaya*. Chotero, ndiye, ngati inu muti mudzakazunzidwe mu gehena kwanthawizonse ndi kwanthawizonse, inu muyenera kukhala muli nawo Moyo Wamuyaya.

³⁰⁴ Koma, tsopano, ine ndiri kukhulupirira kuti Baibulo limaphunzitsa za gehena weniweni wowotcha. Baibulo limaphunzitsa zimenezo, kuti machimo ndi uthakati zidzalangidwa, kwanthawizonse ndi kwanthawizonse. Uwo si Muiyaya, tsopano. Izo ndi mwinamwake kwa zaka mabilioni khumi. Izo zikhoza kukhala kwa zaka mabilioni zana, koma nthawiyina izo ziyenera kudzakhala ndi mathero. Pakuti, chirichonse chomwe chinali ndi chiyambi, chiri ndi mapeto. Ndi zinthu izo zomwe ziribe chiyambi, izo ziribe mapeto.

305 Inu mukukumbukira phunziro limenelo tsopano? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Momwe ife tinapitira mmbuyo ndipo tinapeza kuti chirichonse chomwe chinali ndi chiyambi chinali chopotozedwa, mukuona, kupotozedwa kuchokera ku chenichenicho. Ndipo, potsiriza, izo zikuthera kubwereranso ku Umuyaya. Ndiyeno gehena yense, kuzunzika konse, ndi kukumbukira konse kwa zoterozo, zidzakhala zitatha kwa Muyaya. Chirichonse chomwe chimayamba, chimatha.

306 Ndipo Melkizedeki uyu sanali Yesu, chifukwa Iye anali Mulungu. Ndipo chimene chinamupanga Yesu ndi Mulungu kusiyana, nkuti, Yesu anali kachisi yemwe Mulungu ankakhalamo. Mukuona? Tsopano, Melkizedeki. Yesu anali nawo onse abambo ndi amake. Ndipo Munthu uyu analibe konse bambo kapena amayi. Yesu anali ndi chiyambi cha moyo ndipo Iye anali ndi mathero a moyo. Munthu uyu analibe abambo, analibe amake, analibe chiyambi cha masiku kapena mathero a moyo. Koma, Iye anali Munthu yemwe yemweyo, iye anali. Melkizedeki ndi Yesu anali Mmodzi; koma Yesu anali thupi lapadziko lapansi, lobadwa ndi kupangidwa motsatira tchimo. Thupi lake lomwe la Mulungu, mwana Wake yemwe, wobadwa ndi kupangidwa motsatira tchimo, kuti adzatenge mbola kuichotsa mu imfa, kuti alipire dipo, ndi kuti awalandire ana aamuna ndi aakazi kwa Iyemwini. Inu mukuzimvetsa izo? Ndicho chifukwa choti Iye anali—Iye anali ndi chiyambi, Iye anali ndi mathero.

307 Koma thupi langwiro ili, mu kukumbukira, mo—monga chikole cha chiukitsiro chathu, Mulungu sakadalola thupi loyera ilo kuti liwone chivundi, chifukwa Iye analilenga ilo Mwiniwake. Ndipo analibala ilo, ndipo analiukitsa ilo, ndipo analikhazika ilo pa dzanja Lake lamanja.

308 Ndipo, lero, Mzimu Woyera umene unaliukitsa thupi limenelo uli muno mu Mpingo. Lodala likhale Dzina la Ambuye! Ndipo likusonyeza zozizwitsa zomwezo ndi mphamvu. Ndipo tsiku lina Mzimu Woyera uwu, umene uli mu Mpingo, udzafuula ndi kukwera mmwamba, ndipo udzadzilandira wokha mu mawonekedwe a thupi ili lomwe liri ku dzanja lamanja la Ufumu wa Mulungu, kuti azipanga chitetezero kwa ife ochimwa. Ndipo mwa Ilo ife tikutetezedwa mwangwiro kwa tchimo. Sikuti ife sitimachimwa; koma timatetezedwa kwa tchimo, mu Kukhalapo kwa Mulungu. Chifukwa, pali nsembe Yamagazi ikuima pakati pa ine ndi Mulungu, pakati pa inu ndi Mulungu. Ndi chifukwa Iye anati, “Munthu yemwe wabadwa mwa Mulungu, samachita tchimo, iye sangathe kuchimwa.” Pakuti, ngati iwe wabadwa mwatsopano, Mzimu Woyera womwewo umene unkakhala mu Thupi limenelo ukukhala mwa iwe. Ndipo Iwo sungathe kuchimwa; nsembe ili patsogolo pa Iye. Ndiye ngati iwe uchita izo mwadala, zikusonyeza kuti ndi kosatheka kuti iwe ukhale uli mu Thupi limenelo. Ameni. Ndiwo Uthenga. Ndi Umenewo apo.

³⁰⁹ Chotero, inu mukuona, Izo sizikutsutsana ndi aliwonse a Malemba. Izo zikuwamanga Malemba palimodzi. Mukuona? “Kungakhale kosatheka kwa iwo omwe anawunikiridwapo.” Apo ndi pamene ife titi tipezere mafunso anga. Pakuti, ingowatengani iwo, ndi momwe ife tikufunira.

³¹⁰ Tsopano zindikirani. “Ndi kosatheka kwa iwo omwe anaunikiridwapo, kuti agwe kuti adzikonzenso okha ku kulapa, pakuona kuti iwo akumupachika Mwana wa Mulungu kachiwiri, ndi kumupangitsa Iye . . . ndi kumubweretsa Iye ku manyazi apoyera.” Iwo sangakhoze kuzichita izo.

³¹¹ Ndiye inu pitirirani mpaka ku Ahebri 10, pamene Iwo akuti apo, “Pakuti ngati ife tichimwa mwadala titalandira kale chidziwitso cha Choonadi.” Ndipo kodi tchimo ndi chiani? Kusakhulupirira.

³¹² Ngati inu mwadala mukuwuwona Mzimu Woyera ukuchita zinthu zomwe Iwo unachita pano pomwe mmawa uja, ndi kuwona kuti Khristu wawuka kwa akufa, ndipo Iye akukhala mu Mpingo Wake ndi pakati pa anthu Ake, ndipo inu mwadala nkuwukana Iwo, ndi kosatheka kuti inu mudzabwere konse kwa Mulungu, chifukwa inu mwachitira mwano Mzimu Woyera.

³¹³ Yesu ananena zinthu zomwezo, pamene Iye anali kuchita zozizwitsa zimenezo.

³¹⁴ Iwo ankati, “Bwanji, Iye ndi Bezezebule. Iye ndi wambwebwe. Iye ndi mdierekezi.

³¹⁵ Yesu anapotoloka apo, ndipo anati, “Ine ndikukhululukirani inu chifukwa cha izo. Koma pamene Mzimu Woyera udzabwera ndi kudzachita izo, kudzayankhula mawu owutsutsa Iwo sizidzakhululukidwa konse mu dziko lino kapena mdziko likudzalo. Chifukwa inu mwawutcha Mzimu wa Mulungu umene unali mwa Iye, ‘mzimu wosayera.’”

³¹⁶ Ndiye, ngati ife tichimwa mwadala, ngati ife tichimwa, kusakhulupirira mwadala. Osati titalandira kale Choonadi, kukhala titabadwa kachiwiri; ife sitikanakhoza kuchimwa apo. Wochimwa sangakhoze kuchita losakh- . . . Mkristu sangathe kuchita tchimo losakhululukidwa. Iye sangathe kuchita izo. Ndi opanda umulungu amene amachita zimenezo. Ndi odzipangitsa-kukhulupirira, osati wokhulupirira.

³¹⁷ Arabbi Achiyuda aja, o, iwo ankaganiza kuti iwo anali okhuthara, ndipo iwo anali ndi ma D.D. ndi ma Ph.D. Iwo ankaganiza kuti iwo anali atazisokera izo, mu thumba, koma iwo anali ochimwa oyipisitsa. O, iwo mwina . . . Iwe sukanakhoza kuika dzanja pa iwo, pa moyo wawo. Iwo anali oyer, amakhalidwe, ndi olungama, mwanjira imeneyo. Koma iwo anali osakhulupirira.

³¹⁸ Ndipo inu mukatenga mawu okuti tchimo ndi kufufuza chomwe iwo amatanthauza. Mawu okuti *tchimo* amatanthauza

“kusakhulupirira.” Pali magulu awiri okha, awo ndiwo, wokhulupirira kapena wosakhulupirira. Ndiwo, munthu wolungamitsidwa kapena wochimwa. Ndizo zonse. Ngati inu muli wosakhulupirira, ndinu wochimwa; ziribe kanthu momwe inu muliri wabwino, kuchuluka kwa momwe mumapitira ku tchalitchi, kapena ngakhale ngati inu muli mlaliki. Ndinu wosakhulupirira apobe.

³¹⁹ Afarisi aja anali alaliki, ndipo iwo anali osakhulupirira, ndipo ali mu hade lero chifukwa cha izo. Achipembedzo basi momwe iwo akanatha kukhala ali, ndi achipembedzo, koma iwo sanali kumukhulupirira Iye. Ndipo iwo ankamutcha Iye “mdierekezi,” ndipo ankatsutsa Mawu Ake. Ndipo ena a iwo anati, “Ngati iwe uli, tsopano tsikapo pa mtandawo. Chita chozizwitsa. Tilole ife tikuwone iwe ukuchita izo.” Wina anamugoda Iye pa mutu, ndi ndodo, ndipo anati, “Nenera ndi kuti iwe ife yemwe anakumenya iwe, iwe mneneri, ndipo ife tikukhulupirira iwe.” Mukuona, osakhulupirira! Iwo ankadzipangitsa kukhulupirira kuti iwo anali okhulupirira, koma iwo anali osakhulupirira, osasinthika, olekanitsidwa, ngakhale iwo anali oyera ndi achipembedzo.

³²⁰ Komabe, icho ndi chinthu chomwecho chimene chikuima lero. Amuna ndi akazi akukhoza kumapita ku mpingo ndi kukakhala ndi nkhope zazitali, n—ndi mwachipembedzo momwe iwo akanakhala aliri, ndi kusamanama konse, kuba, ndi kumayesera kukhala moyo wa chipembedzo chawo mopambana momwe iwo angathere. Koma, kupatula ngati iwo ali okhulupirira, iwo ataika. Koteri mulibe pang’ono pa azamwalamulo mu Baibulo. Chikalvini ndi... Chisomo ndi chimene Mulungu anakuchitirani inu, ndipo ntchito ndi zomwe inu mumamuchitira Mulungu. Izo ziri mwamtheradi zolekanitsidwa.

³²¹ Ngati inu mukanasiya kunama, mukanasiya kusuta, mukanasiya kuba, kusiya kuchita chigololo, kusiya zonse, mutachita chirichonse, mutasunga malamulo, ndipo mumapita ku mpingo, kumabatizidwa Lamlungu lirilonse, kudya mgonero, kusambitsa mapazi a oyera, mutachita chirichonse, kuchiza odwala, ndipo mutachita zinthu zina zonse izi, kupatula ngati inu mutabadwa mwa Mzimu wa Mulungu, mutasankhidwa, inu mwataika. “Si iye amene afuna kapena iye amene athamanga, koma Mulungu yemwe amasonyeza chifundo.”

³²² Esau anayesera mwakukhoza kwake kuti akhale Mkhristu, ndipo sanakhoze kuchita izo. Baibulo linati iye analira mowawa, akufunafuna malo oti alapirepo, ndipo sanakhoze kuwapeza iwo. Iye asanabadwe nkomwe, Mulungu anamuweruza iye, chifukwa iye ankadziwa kuti iye anali tambwali wovunda mu mtima mwake. Mulungu mwa kudziwiratu anazidziwa izo. Iye anati, “Ine ndikumukonda Yakobo, ndipo ine ndikumuda Esau.” Ndipo Esau ankawoneka ngati njonda. Iye ankakhala

kunyumba, ankawasamalira abambo ake okalamba akhungu, ankadyetsera ng'ombe, ndi chirichonse, anali mnyamata wabwino.

³²³ Ndipo Yakobo anali mwana wa amayi, wonena nthano wamng'ono wachikazi. Ndi chimene iye anali. Inu muyenera kuvomereza izo. Baibulo limavomereza, limabweretsa izo. Ankayendayenda, kumachita chirichonse. N—ndipo, amayi, kumakhala pafupi ndi amayi. Koma, apobe, Yakobo, ali nazo zokwera ndi zotsika zakezo, ndi njira zake zachikazi, iye anali nakobe kulemekeza kwa ufulu wa kubadwa uja. Ndiko kayimbidwe koyamba.

³²⁴ Esau anali nazo pawiri unjonda wa Yakobo. Ngati ife tikanati timuweruze iye lero, kuti akhale membala wa mpingo wathu, inu mukadamutenga Esau, chikwi kwa mmodzi, ngati inu mukanati musamudziwe iye. Koma Mulungu anatenga Yakobo.

³²⁵ Inu mukanachita naye chiani Paulo Woyera, ngati iye akanafuna kuti akhale mtumiki? Myuda wamng'ono, wa mphuno ya ngowe, ndi kamwa yopotolozekera chammbali, akupita motsatira akungochita ukali, ndi momwe amapitira kukauphwasula Mpingo. Iye amapita kukachita chirichonse. Inu mukanaganiza kuti iye anali atachimwa tchimo losakhululukidwa. Koma Mulungu anati, “Iye ndi wantchito wanga.”

³²⁶ Mulungu amawatenga anthu ndi kuwapanga iwo mosiyana, osati anthu kumutenga Mulungu ndi kukhala mosiyana. Mulungu amamutenga munthu ndi kumupanga iye mosiyana. Si zimene inu muchita, zomwe inu mufuna, zomwe inu muganiza. Ndi zimene Mulungu achita. Ndi inu apo. Ndipo iyo ndiyo nkhaniyo.

³²⁷ Tsopano, Melkizedeki wamkulu uyu, nkhani yakeyo ya Iye apa! Ife tikufuna kuti tiwerenge pang'ono pokha, choimira ichi. Ife tinachita kuthamanga mu izo mofulumira kwambiri. Ife tiyenera kuyambira mmbuyomu apa pa gawo lina la Lemba, ndipo ife tikuti tiyambire cha pa ndime ya 15.

Ndipo izo ziri apobe...zowoneka kwambiri: kuti apo...pakuti monga mwa mafananidwe a Melkizedeki apo pakuwuka wansembe wina.

³²⁸ Tsopano, Melkizedeki anali wansembe. Anali iye? Apa pali chimene Iye anali. Ife tikupeza kuti Mulungu, pachiyambi, anali kasupe wamkulu wa Mzimu. Ndi kulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Iye analibe malo obadwirapo. Iye analibe malo oferapo. Iye analibe chiyambi cha masiku. Iye analibe mathero a zaka. Iye anangokhala Wamuyaya monga Umuyaya uli Wamuyaya. Iye sanachite kubadwa konse. Iye sanachite kufa konse.

³²⁹ Ndipo mmenemo, ife tikupeza kuti, Iye anali nako kusiyana kusanu ndi kuwiri kwa Mzimu. Ndi kulondola uko? Baibulo

linatero, mu Chivumbulutso, kuti, “Mizimu isanu ndi iwiri ili patsogolo pa Mpando wa Mulungu.” Ndi kulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kasanu ndi kawiri, kufutukuka, kasanu ndi kawiri kwa Mzimu. Ife tikupeza, apo pali milozo isanu ndi iwiri. Apo pali mibadwo isanu ndi iwiri pamene. O, izo zikungoyenda. Seveni ndi kutsirizitsa, ndipo Mulungu anali wamphumphu. Ndipo Mizimu isanu ndi iwiri, ndipo Mizimu imeneyo inali yangwiro. Woyamba unali mtundu wofiira; chikondi changwiro, chiwombolo. Ndi momwe, ngati ife tikanakhala nayo nthawi, kuti tipereke mitundu imeneyo ndi kusonyeza kuti uliwonse wa mitundu imeneyo ukuimira ungwiro wa Mulungu. Amen. Mitundu imeneyo, ilipo mitundu isanu ndi iwiri yachirengedwe apo. Mitundu imeneyo ikuimira ungwiro wa Mulungu. Ndipo... Mitundu imeneyo ikuimira zomupangitsa za Mulungu, katengedwe kazinthu ka Mulungu. Milozo isanu ndi iwiri iyo, iyo ikuimira mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo, nyenyezi zisanu ndi ziwiri, angelo asanu ndi awiri. Zonse kudutsa mu Lemba, atumiki asanu ndi awiri, amithenga asanu ndi awiri, mauthenga asanu ndi awiri, zonse mu zisanu ndi ziwiri. Masiku asanu ndi awiri. Masiku asanu ndi limodzi, ndipo lachisanu ndi chiwiri ndilo la sabata; zangwiro, zamphumphu. O, ndi zokongola, ngati ife tikadangkhalala nayo nthawi yoti tikumbe mu izo ndi kuzitulutsa izo kunja, mitundu imeneyo!

³³⁰ Kutenga mtundu wofiira. Ife titenge mtundu woyambirira, ndi wofiira. Kodi kufiira ndi chiani? Kufiira ndi chizindikiro chimodzi cha ngozi. Kufiira ndi chizindikiro cha chiwombolo. Ndipo inu mukayang’ana pa chofiira kupyolera mu chofiira, ndi mtundu wanji umene uli? Woyera. Ndiko kukhoza. Chotero pamene Magazi ofiira anakhetsedwa, kuti aphimbe tchimo lofiira; Mulungu, poyang’ana kupyolera mu Magazi ofiira, poyang’ana pa tchimo lofiira, ilo limakhala loyera. Wokhulupirira sangathe kuchimwa. Ndithudi ayi. Mbewu ya Mulungu, madalitso a Mulungu, amakhalabe pa iye. Mulungu sangathe kuwona china koma Magazi a Mwana Wake yemwe. Ziribe kanthu chomwe izo ziri mu Mpingo Wake, chomwe iwo uli, Mulungu samaziwona izo, chifukwa Yesu akupanga chitetezero, mosalekeza, Wansembe Wamkulu. Palibe njira yoti iye achimwire, pamene Nsembe yoteroyo ili apo kwa iye, monga choncho. Ndithudi ayi.

³³¹ Ndipo tsopano ngati inu mukuti, “Chabwino, izo zikundipatsa ine mwayi wabwino...” Ndiye izo zikusonyeza kuti inu simuli moyenera.

³³² Inu muziyamikira Izo. Inu muzizikonda Izo, ngati inu muli Mkhristu weniweni, mpaka pa malo pomwe tchimo likanati lizikuzunzani inu mpaka inu simukanati muzilichita ilo. “Pakuti Mbewu ya Mulungu ikanali mwa iye, ndipo iye sangathe kuchimwa.” Baibulo linati, “Akatsukidwa kamodzi ndi Magazi

a Yesu, samakhala nachonso chilakolako cha tchimo.” Ngati inu muli ndi chilakolako, mtima wanu suli moyenera ndi Mulungu.

³³³ Tsopano, inu muzilakwitsa, koma inu simumazichita izo mwadala. Mukuona? I—inu mwatcheredwa msampha, ndipo chirichonse chimene inu mwatcheredweramo, kapena kuchita chinachake chimene inu simumatanthauza kuti muchichite, icho si tchimo apobe, inu mulapa miniti yomwe inu muti muwone kuti inu mwalakwitsa. Inu mudzapotoloka mwamsanga ndi kuti, “Ine sindimatanthauza . . . sindinachiwone icho.” Inu mukhala mukunena izo, kudutsa mu moyo wonse. Munthu samafuna kuti akhale, ndicho chifukwa ife tiri opusa kwambiri ndi a mumdima kwambiri, pansu pano mu dziko, kuti pali chitetezero cha Magazi kwa ife, nthawizonse, chomwe chimakhala chikutiphimba ife. Chifukwa, kulakwitsa koyamba komwe ife tinakomana nako . . .

³³⁴ Tsopano, ilo ndi lingaliro lanu lamwalamulo. “O, inu mukudziwa chiani? Mkazi uyo anali woyeretsedwa. Koma, adalitsidwe Mulungu, iye wachita cholakwika. Ine ndikudziwa iye wabwerera mmbuyo.” Uko ndi kulakwa. Iye sanabwerere mmbuyo. Iye wapanga cholakwitsa. Ngati iye anachichita icho mwadala, ndiye iye sanali molondola, pa kuyamba pomwe.

³³⁵ Ngati iye samatanthauza kuti achite icho, ndipo iye anayenda napita patsogolo pa Mpingo woyera wa Mulungu ndi kuchivomereza icho, ndi kuti, “Ine ndalakwitsa, ndipo inu ndikhululukireni ine,” inu muli okakamizidwa kuti muchite izo. Inu mukapanda kuchita izo mu mtima mwanu, ndiye inu muyenera kuti mupite ku guwa inueni. Zoona. Ndi chimenecho chiyero chenicheni mu mpingo. Apo pali chiyero chenicheni, chiyero osati cha inu, koma cha Khristu.

³³⁶ Ine ndiribe chiyero choti ndichipereke kwa Iye. Koma ine ndikudalira mu Chakecho, o, chisomo Chake, ndipo ine ndiri nacho icho mu mtima mwanga. Ine sindinachipindule icho, palibe chimene ine ndingati ndichite kuti ndiyenere icho, koma mwa chisomo Iye anandiitana ine ndipo anandiitanitsa ine kuti ndibwere. Ndipo ine ndinayang’ana kwa Iye, ndipo Iye anandichotsera chikhumbo kutali ndi ine. Ine ndimapanga zolakwitsa zikwi mu mwezi uliwonse, mu chaka chirichonse. Zedi. Ine ndimatero. Koma pamene ine ndiwona kuti ndalakwitsa, ine ndimati, “Mulungu, ine sindimatanthauza kuti ndichite izo, Inu mukuwudziwa mtima wanga. Ine sindimatanthauza kuti ndichite izo. Ine ndinatchedwera msampha mu izo. Ine sindimatanthauza kuti ndichite izo. Inu mundikhululukire ine, Ambuye.”

³³⁷ Ngati ine ndachita chomulakwira m’bale wanga, ine ndimati, “M’bale, ndikhululukire ine. Ine sindimatanthauza kuti ndichite izo.” Ndithudi, Mulungu akudziwa mtima wanga.

³³⁸ O, ndi inu apo. Ndi imeneyo nsembe ya Magazi. Ndi imeneyo mphamvu ya Uthenga, Mpingo woyera uwo ukupita patsogolo.

Osati chifukwa cha chinachake chimene inu mwachita; ndi chinachake chimene inu munalibe kanthu kochita nacho. Ndi chimenecho Chitetezerocho.

³³⁹ Tsopano, Melkizedeki uyu, pamene Iye anabwera apo.

³⁴⁰ Ine ndikufuna kuti ndikuuzeni inu chinthu china. Kodi inu munayamba mwatengapo—chidutswa cha galasi cha mbali zitatu? Inu mukatenga chidutswa cha galasi cha mbali zitatu, ndi kuchiika icho mwakuti dzuwa liziwomba pa icho, ilo lizitulutsa mitundu isanu ndi iwiri yangwiro. Chidutswa cha galasi cha mbali zitatu chimatulutsa utawaleza. Ndiko kulondola ndendende. Tsopano, ngati ife tikadakhala nayo nthawi, ife tikadapita mu zimenezo. Zitatu zimabweretsa ungwiro: Atate, Mwana, Mzimu Woyera; kulungamitsidwa, kuyeretsewa, ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndi inu apo. Ungwiro umabwera mwa zitatu. Mulungu, pamwamba pa munthu; Mulungu, mwa Munthu wotchedwa Yesu; Mulungu, mu Mpingo. Ndiyeno, ungwiro.

³⁴¹ Munthu ankachimwa, utali wonse pamene Mulungu anali pamwamba *apa* mu Lawi la Moto, Mulungu. Munthu anachimwa, kani, pamaso pa Mulungu, utali wonse pamene Mulungu anali mu Lawi la Moto, chifukwa iye anali cholengedwa chosayera apabe, magazi a nyama anali patsogolo pa Iye.

³⁴² Kenako Mwanawankhosa wa Mulungu anabwera, sitepe yachiwiri yotsimikizika ya Mulungu; Mulungu yemweyo, udindo wina. Ndiyeno Mulungu uyu m...anali mwa Khristu, anali Mulungu yemweyo amene anali mu Lawi la Moto. Ndipo Mulungu yemweyo anapangidwa thupi ndipo anadzakhala pakati pathu. Ndiyeno anthu ankamunyogodola Iye, iwo apobe anali akuwerengedwerabe chifukwa cha izo. Apo panali popanda Magazi atakhetsedwa apobe. Ndiko kulondola. Yesu anati, “Ine ndikukhululukirani inu.”

³⁴³ Komano Mmodzi yemweyo amene anali mnofu, anakhala wa mu Lawi la Moto kachiwiri. “Ine ndinabwera kuchokera kwa Mulungu. Ine ndikupita kwa Mulungu.” Apa ife tikupeza Paulo akukomana ndi Iye, pa njira waku Damasiko, Lawi la Moto lomwelo. Ife tikupeza Petro akukomana naye Iye mu ndende, Lawi la Moto lomwe lija. Ndithudi. Ndipo ife tikumuwona Iye lero, pakati pathu, Lawi la Moto lomwelo.

³⁴⁴ Koma ungwiro wafika pa malo, kuti munthu wapakati... Tsopano, ngati zitachitika kuti pali Myuda pano, kapena winawake yemwe amamvetsa Chipangano Chakale. Kutsimikizira izo, ndiloreni ine ndikusonyezeni inu. Ine ndiribe Chipangano Chakale limodzi nane, pakali pano. Ichi n—ndi Chipangano Chatsopano. Koma mu kupereka nsembe kwa mkate wopanda chotupitsa womwe unkakhala pa mbale yopatulika, mu nsembe ya Chiyuda pa kuyeretse kwa makachisi;

mufunzeni Myuda aliyense; pa zidutswa zitatu za mkate izo, chidutswa chapakati chinali chonyemedwa. Ameneyo anali Khristu. Chidutswa chapakati chinali chonyemedwa; Khristu, wa pakatipo. Zinkasonyeza kuti pankayenera kudzakhala kunyema, penapake, kwa chiwombolo. Ndipo chidutswa chimenecho chinkawerengedwa ngati chiwombolo, pa mkate wopatulika.

³⁴⁵ Ndipo apa Iye ali. Ndipo usikuuno, pamene ife tizidya mgonero, ife timanyema mkate wopatulika, pakuti ilo ndi thupi la Khristu. Ndipo Iye ananyemedwa pa Kalvare, kuti akhale chitetezero cha machimo athu, kuti kupyolera ma chirungamo Chake ife tikhoze kukhala chilungamo Chake. Chifukwa, Iye anakhala tchimo lathu, kuti ife tikhoze kukhala chilungamo Chake. M'bale, ndicho chisomo mwanziro. Mwamtheradi. Palibe njira, njira ina iliyonse yomwe mukanati muzilungamitsire.

³⁴⁶ Tsopano, Melkizedeki uyu, Munthu wamkulu uyu yemwe anakomanizidwa pa njira. Iye analipira, Abrahamu analipira zachikhumi kwa Iye. Kukula kwake kwa Munthuyu komwe Iye ayenera kukhala ali! Tsopano zindikirani, mwamsanga.

*Yemwe anapangidwa, osati mosatidza lamulo la . . .
malamulo achithupithupi, . . .*

³⁴⁷ Tsopano mukuona lamulo lamwalamulo ilo? Lamulo linkati, "Iwe usati uzipha. Iwe usati uzichita chigololo. Iwe usati uziba."

³⁴⁸ Yesu anatembenuka apo mmbuyo momwe, anati, "Kunanenedwa ndi iwo a nthawi zakale, 'Iwe usati uzipha,' koma ine ndikuti aliyense yemwe akwiya naye m'bale wake, popanda chifukwa, wapha kale. Kunanenedwa ndi iwo, a nthawi zakale, 'Iwe usati uzichita chigololo,' koma ine ndikuti kwa inu, aliyense yemwe ayang'ana pa mkazi mpaka kumusilira iye, wachita chigololo kale mu mtima wake ndi iye." Ndi inu apo. Izo zikuyenera kuwaphunzitsa akazi momwe angamavalire, momwe angamachitire zomwe ziri zoyenera. Inu mumavala molakwika, ndipo mumawapangitsa amuna kuti azikuyang'anani inu mwanjira yolakwika, inu muli olakwa pakuchita chigololo, chimodzimidzi basi ngati kuti inu munadutsa mu kachitidweko. Yesu ananena chomwecho.

³⁴⁹ Ndipo inu anthu a kupsya-mtima kwa macheka uku, omwe nthawizonse mumakhala mukukhavukira mkamwa pa winawake, osatha kudziletsa, ndi zinthu monga izo. Khalani osamala. Ndinu olakwa ngati inu muyankhula mawu (motsutsa m'bale wanu) izo si zoyenera, si zolungama, kupita mozungulira ndi kumaphwasula izo. Inu simumasowa kumubaya kumbuyo munthu kuti mumuphe iye. Inu mukhoza kuswa khalidwe lake ndi kumupha iye, kupha chikoka chake. Kuyankhula motsutsa m'busa wanu pano, kunena chinachake choipa chokhudza iye, inu mukanangokhala ngati kuti mwamuwombera iye.

Mwanena chinachake chimene sichinali choyenera chokhudza iye, chabwino, izo zipha kukopa kwake kwa anthu ndi zinthu zonga izo, ndipo ndinu olakwa pa izo. Zomwe Yesu ananena.

³⁵⁰ Tsopano, mvetserani apa, zo—zomwe Paulo anali kuyesera kuti afike pa icho apa. Ine ndimalikonda Baibulo lachikale ili. Ilo limakuwongola iwe. Penyani, o, tangoyang’anani apa. Tsopano, pamene ife tikuwerenga yachinai- . . . “Iyo ili . . . pakuti ndi chodziwika kuti Ambuye wathu anachokera kwa Yu- . . .” Dikirani, ine ndikukhulupirira ine ndiri ndi ndime ina apa yomwe ine ndimati ndiiwerenge. Ayi, pansi apa pa ya 16.

Yemwe anapangidwa, osati motsatira lamulo la . . . lamulo lachithupithupi, . . .

³⁵¹ Izo ndi zamwalamulo, inu mukuona. “O, m’bale, i—ine ndisatero. Ine ndisatero. Ine ndikudziwa, koma i . . .” Sindizo ayi. Ndi chikondi chimene chimachita izo.

³⁵² Momwe ife tinadutsira mu izo! Ine ndinati, “Ngati ine ndikananena kwa wanga . . . za mkazi wanga, ‘O, chabwino, i—i—ine ndikanakonda kuti ndikhale ndi akazi awiri. Ine ndikanakonda kuti ndiziyendayenda ndi *uyu*, kuchita ndi *uyu* uko. Koma, ngati ine nditero, mkazi wanga andisudzula ine . . . Ndipo ana anga akhala mu . . . Utumiki wanga utaika.” Iwe wauve wachinyengo, wovunda. Ndiko kulondola. Iwe sukumukonda iye molondola, pa malo oyamba. Ndiko kulondola ndendende.

³⁵³ Ngati iwe ukanati uzimukonda iye, apo sipakanakhala lamulo la izo. Iwe ukanati uzimukonda iye, mulimonse, ndipo iwe ukanamamatirana naye iye. Ndizo ndendende kulondola. Ndipo inu akazi muzichita chinthu chomwecho kwa amuna anu. Ndiko kulondola.

³⁵⁴ Nthawizina akazi amakhaka malo, kapena . . .

³⁵⁵ Mwamuna akawona Yezebeli wina wamng’ono atazilocha yense, inu mukudziwa, n—ndipo iye amapita uko, kugwa chifukwa cha iye; mwinamwake mkazake ali wabwino. Ndiyeno inu mumadzitcha nokha Mkhristu. Manzayo pa inu. Inu mukusowa mankhwala ena a pa guwa. Ndiko kulondola.

³⁵⁶ Ndipo ena a inu—ndipo ena a inu akazi mumayang’ana apo pa kamnyamata kena kachikulire kali ndi tsitsi lake lopesedwera pansu, Vaselini wokwanira ali pa ilo kuti atsegule kamwa yake. Ndiyeno inu . . .

³⁵⁷ Kamsungwana kena kachikulire, kuno osati kale litali. Iyi si nthabwala, chifukwa ine sindikutanthauza kuti ndinene izo ngati nthabwala. Koma anthu akudziwa kuti ano si malo a nthabwala. Koma kamsungwana kachikulire kuno, iye . . . Panali anyamata abwino kuno, anyamata Achikhristu. Nthawi yaitali yapitayo, pamene ine ndinkachita ubusa kuno, ife tinkakonda kukhala ndi makalasi a anyamata okha. Ndipo ine

ndinkayankhula ndi akazi aang'onowo Lamlungu madzulo, pa za kugonana ndi zinthu. Ndiye Lamlungu lotsatira madzulo, nkuyankhula kwa amuna aang'ono, ndi kuyesera kuti tizifikitse zinthu izo powongoledwa.

³⁵⁸ Kamsungwana kena kachikulire kanayamba kumapita ndi kachinkhanira kena kachikulire, kumzinda wakale kuno, ankasuta ndudu ndipo ankakhala ndi kamkunda mthumba mwake. Ndipo iye ankayendetsa galimoto yang'ono ya roadster kuzungulira mzindawo. Ine sindinkakhoza kuwona zomwe iye ankawona mwa mnyamata ameneyo. Iye sankabwera ku tchalitchi. Iye ankakhala panja apo. Kumuyika iye mu tchalitchi muno, ndiyeno iye ankakhala panja uko, mu galimoto yake, ndi kumamudikira, sankakhoza kubwera mu tchalitchi. Ine ndinanena kwa iye tsiku lina. Iye ankakhala mu New Albany. Ine ndinati, “Ine ndikufuna ndikufunse iwe chinachake, msungwana. Ndi chiani mu dziko chomwe iwe umawona mwa mnyamata ameneyo?” Ine ndinati, “Malo oyamba, iye amadana nacho chipembedzo chomwe chimene i—iwe uli nacho. Iye amamunyoza Khristu wako. Iye sangadzathe konse kukupangira iwe mwamuna wako. Iye angadzakupangitse iwe kukhala womvetsa chisoni, moyo wako wonse.” Ndipo ine ndinati, “Chabwino, kuli anyamata abwino Achikhristu kuno omwe ukanamakhoza kumayenda nawo. Ndipo apo bambo ako ndi amayi amadana nawo maganizo okuti iwe uzipita kwina, koma iwe umapita mulimonse, ndipo iwe ukuganiza, ‘Ndine wokoma wa sikisitini.’”

³⁵⁹ Iye anayamba kumadzilocha ndi kumathamangira kunja, ndipo chinthu choyamba, iye anali mu nyumba za kumsewu. Iye anapita kale ku Umuyaya tsopano. Koma, ndiye, iye anama apa. Ndipo inu mukudziwa chowiringula chimene msungwana ameneyo anandipatsa ine kumbuyo uko, kuti iye ankamukonda mnyamata ameneyo? Iye anati, “Iye ali ndi mapazi aang'ono okongola chotero, ndipo iye amanunkhira bwino kwambiri.” Kodi inu mungakhoze kulingalira zimenezo? Kuzitsira yekha zodzinunkhiritisa, ameneyo ndi wachikazi, osati mwamuna.

³⁶⁰ “Taonani,” ine ndinati, “mlongo, ine kunalibwino ndiziyenda ndi mnyamata wa Chikhristu yemwe ali ndi mapazi ngati zimagalimoto zodiriza msewu ndi kumanunkha ngati kanyimbi, ngati iye anali Mkhristu mwamtheradi.” Ndiko kulondola. Zoon. Eya.

³⁶¹ Ndi chowiringula, “Mapazi okongola aang'ono choterowo, ndipo amanunkhira bwino kwambiri.” Wamng'ono wothamangira kunyumba za kumsewu, potsiriza anawononga moyo wa mtsikanayo. Ndi zamanyazi, zopandachisomo.

³⁶² Ukwati ndi wolemekezeka, koma iwo uyenera kuti uzilowedwa mopempherera ndi molemekeza. Ndipo chikondi chenicheni kwa mkazi ameneyo chidzakumangirizani inu

palimodzi kwanthwizonse. “Chimene inu muchimanga pa dziko lapansi, ine ndichimanga Kumwamba.” Pamene inu mukuyenda pansu mu msewu uko, iye akhoza kukhala wokalamba ndi waimvi ndi wamakwinya, koma chikondi chomwecho chimene iwe unali nacho kwa iye pamene iye anali mkazi wamng’ono, wokongola, iwe udzakhala uli nachobe icho.

³⁶³ Iwe ukhoza kugwa mapewa, wamutu-wadazi, ndi nkhope yamakwinya ndi china chirichonse, koma iye azidzakukonda iwe basi monga iwe unkachitira pamene unkauma ndi mapewa otambalala ndi tsitsi la mzindo, ngati ali Mulungu kwenikweni. Pakuti inu mukuyang’ana ku nthawi pamene inu muti mudzawoloke mtsinje kutsidyako, pamene inu muti mudzatumphukire, kachiwiri kukakhala mnyamata ndi msungwana, kukakhala moyo limodzi kwanthawizonse. Ndilo lonjezo Lamuyaya la Mulungu. Iye anati Iye akanati adzazichite izo. Iye, si izo zokha...Ife tifika kwa izo mu miniti. Iye analumbira kuti Iye akanati adzazichite izo.

³⁶⁴ Mvetserani kwa izi, pamene ife tiri kupitirira.

*Yemwe anapangidwa, . . . motsatira lamulo la . . .
malamulo achithupithupi, koma motsatira mphamvu
ya . . . moyo wopanda mapeto.*

³⁶⁵ Tsopano ife tikuti tiwerenge mofulumira, chotero kuti ife tikhoze kuzimvetsa izo.

*Pakuti iye akuchitira umboni, Inu ndinu wansembe
kwa nthawizonse mwa dongosolo la Melkizedeki.*

Utali wonse pamene pazifunika wansembe, Iye akhala ali wansembe.

*Pakuti pali umboni kuthetsa kwa lamulo kupita
patsogolo . . . kufooka kwa chosapindulitsa chakecho.*

*Pakuti lamulo silinapange kanthu kena kukhala
kangwiwo, . . .*

³⁶⁶ Inu simungathe, ziribe kanthu zomwe inu muchita. Inu mukasiya kumwa, mukasiya kusuta, kusiya kunena mabodza, kumapita ku mpingo ndi kuyesera kumachita izi ndi kuyesera kumachita izo, inu mukanali wachithupithupi. Ilo ndi lamulo chabe. Lamulo silimapangitsa kanthu kena kukhala kangwiwo. Koma nchiani chimapangitsa kukhala changwiwo? Khristu. Ulemerero! Ine ndikhoza kusiya kunena bodza, kusiya kuba, kusiya kuchita chigololo, kusiya kutafuna, kusiya zinthu zonse, ndipo ine ndikadali wachithupithupi. Mulungu samazilandira izo, chifukwa ine ndiribe kanthu koti ndingamupatse Iye mwa chitetezero.

³⁶⁷ Koma miniti yomwe ine ndinayika manja anga pa mutu wodala wa Ambuye Yesu, ndi kuti, “Ambuye, sindine wabwino. Kodi inu munganditenge ine ngati wantchito Wanu?” ndipo Mulungu amapsyopsyona nawachotsapo machimo anga, ine

ndimaima wangwiro pamaso pa Mulungu. Ndiko kulondola. Bwanji? Ine sindikuima pa kuyenera kwanga kwanga. Ine ndikuima pa Kwake. Ndipo Iye anatipanga ife kukhala angwiro, kupyolera mu kuzunzika Kwake ndi Magazi Ake.

³⁶⁸ Ine ndikuwona kuti ndi nthawi yoti titseke. Koma ine ndikufuna kuti nditsirize kuwerenga izi ngati ine ndingathe, mwamsanga.

...kupita patsogolo pakuti chifooko ndi chosapindulitsa pamenepo.

Pakutitu lamulo silinapange kanthu kena kukhala kangwiro, koma kubweretsa umo kwa chiyembekezo chabwinoko kunatero; (Kodi chiyembekezo chabwinoko ndi chiani? Khristu.) chimene tiyandikira nacho kwa Mulungu.

³⁶⁹ Bwanji? Kupyolera mu ubwino wathu wonse, ndi ubwino wathu wonse, ndi ubwino wathu wonse, ife tikadali achithupithupibe. Koma tikangokhala kamodzi mu kukhalapo kwa Mulungu, kuzindikira kuti ife sitingakhoze konse kuima pamenepo, kupatula kudzera mu kutiyenereza kwa Yesu Khristu, ndiye ife timayandikira kwa Mulungu, kudzera mu kutiyenereza kwa Mwana Wake. “Ambuye, ine ndikudza kwa Inu, ndi mtima wosalakwa. Mu Dzina la Mwana Wanu Yesu, chonde ndilandireni ine.” O, m’bale, inu mukubwera mwa njira yamoyo ndiye.

³⁷⁰ Osati, “Ambuye, Inu mukudziwa ine ndinasiya kumwa. Inu mukudziwa ine ndimamuchitira mkazi wanga zoyenera. Inu mukudziwa ine ndimachita izi. Ine ndimachita izo.” Inu mulibe kanthu koti mungakapereke.

³⁷¹ “Pakuti lamulo la malamulo achithupithupi silikanakhoza kuchita kalikonse, koma kubweretsa umo kwa chiyembekezero china kunatero. Chiyembekezo icho chomwe chiri Khristu, ife tiri nacho monga nangula wa moyo, woima njii ndi wotsimikiza.” Penyani.

Ndipo mochuluka chotero monga osati popanda lumbiro iye...

Puronauni, ngati inu muti muzindikire umu, mu zolemba zazing’ono.

...iye anapangidwa kukhala wansembe:

Osati kokha wansembe, koma Iye anapangidwa kukhala wansembe mwa lumbiro. Osati...

³⁷² Tsopano penyani. Tiyeni titenge unsembe wina wonse.

(Pakuti ansembe aja, Achilevitiko, olungama, olungama, amuna owonamtima, ansembe awo anali kupangidwa popanda lumbiro;...)

³⁷³ Mulungu anangoti, “Motsatira dongosolo la—motsatira dongosolo la Aroni, momwe iye ankawapangira ansembe awa.” Iwo ankabwera kudutsa mu timbadwo, ndi kupita ku sukulu ndi kukaphunzira kuti akhale alaliki ndi zina zotero. Iwo ankabwera nazo. Kotero Mulungu ankawapanga iwo kukhala ansembe monga chomwecho. Iwo ankadzipanga okha kukhala ansembe, mwa maphunziro awo, mwa cholandira chawo, ndi zina zotero. “Koma Munthu uyu anapangidwa kukhala wansembe mwa lumbiriro limene Mulungu analipanga.” Mvetserani mwatheru tsopano.

(. . . anali kupangidwa popanda lumbiriro; koma uyu ndi lumbiriro mwa iye amene anati kwa iye, Ambuye alumbira ndipo sadzalapa, ameni, Iwe ndiwe wansembe kwanthawizonse motsatira dongosolo la Melkizedeki.)

Mwa zochuluka chomwecho Yesu anapangidwa chitsimikiziro cha pangano labwinoko.

Tsopano, mwamsanga.

Ndipo iwo moonadi anali ansembe ambiri, chifukwa iwo sanali kuloledwa kuti azipitirira mwa chifukwa cha imfa:

Zikwi kuchulukitsa ka zikwi zikwi, za ansembe, chifukwa iwo analibe kalikonse koma imfa yokha ndi imfa ndi zifooko, ndi imfa ndi imfa ndi imfa.

³⁷⁴ Koma mpenyeni Iye.

Koma munthu uyu, (munthu uti?) Yesu, chifukwa iye mopitiriza akupitirira nthawizonse, ali nawo unsembe wosasintha. Komwe ali . . .

Chomwechonso iye ali wokhoza aponso kuwapulumutsa iwo mpaka kutalitali; ziribe kanthu kutalikira kwake, kutsika kwake, kutalikira kwake chotani, iye ali wokhoza kupulumutsa mpaka kutalitaliko; omwe adza kwa Mulungu mwa iye, . . .

Sikuti zinali pa chilungamo chanu; koma pa kuvomereza kwanu. Mukuona?

. . . omwe adza kwa Mulungu mwa iye, powona kuti iye akukhalabe moyo nthawizonse kuti aziwapangira iwo chitetezero.

Iye ali apo pomwe, mosalekeza, kupanga chitetezero.

Kuchokera kwa wansembe wamkulu woteroyo zinatiyenera ife, omwe tiri oyera, osapweteka wina, osaipitsidwa, olekanitsidwa kwa ochimwa, ndi opangidwa kukhala wansembe wamkulu kumwamba;

³⁷⁵ Ndi izo apo. Tsopano, ngati ine ndikanati ndiyesere kuti ndidziimire mulandu wanga womwe, ine ndikanawulephera iwo. Ngati ine ndikanati ndiyesere kuimira, kuti, “Chabwino,

bambo anga anali munthu wabwino. Bambo anga anali mlaliki. Chabwino, ine ndakhala ndiri mu mpingo.” Ine ndikanati ndiwulepherebe iwo. Koma Munthu uyu ndi Mmodzi wangwiroyo, Khristu. Iye akukhala pamenepo ndi kumapereka Magazi Ake mosalekeza kwa machimo anga. Ndi inu apo.

Yemwe samasowa patsiku, monga aja . . . ansembe, kuti aziperekapo nsembe, poyamba kwa machimo ake omwe, ndipo kenako kwa anthu: pakuti izi iye anazichita kamodzi, pamene iye anadzipereka mwiniwake.

376 Tsopano penyani ndime yotsiriza.

Pakuti lamulo limawapanga anthu kukhala ansembe aakulu omwe ali ndi chifooko; . . .

377 Ndi chomwe lamulo, lamulo lachithupithupi, limachita. Tsopano, ine ndikukhumba ine ndikanangokhala nawo pafupi maora awiri apa pomwe. Ndi momwe lamulo likuwapangabe amuna kukhala alaliki. Ndiko kulondola.

378 Bwanji, iwo amati, “Pakutitu, mwamuna uyu ali ndi kudziwa kwa ku seminare.” Ine sindikanati ndigulitse chondichitikira changa chaching’ono chachikale Chakumwambachi pofuna maseminare onse a mu dziko.

379 “Pakutitu, ife tamuphunzitsa mwamuna uyu. Iye n—iye ndi wochita kutengedwa pamanja. Iye ndi munthu wodzipanga yekha.” Ine sindimawukonda mtundu umenewo. Ine ndimakonda munthu wopangidwa ndi Mulungu. Mukuona? Mukuona?

380 Koma lamulo likumawapangabe ansembe. Lamulo likumawapangabe alaliki. M—mpingo wa Baptisti, iwo amapereka kwina alaliki; odzaza mmanja a iwo, ali ndi makina omwe amapukusa nawatulutsamo iwo. Amethodisti ali nawo iwo. Abaptisti ali nawo iwo. Apresbateria, Anazerine, Apilgrim Holiness, Apentekoste, iwo amapukusa nawatulutsa iwo mofulumira momwe iwo angathere, monga ulamuliro wawukulu, makina aakulu. Amaima apo ngati . . .

381 Ine nthawizonse ndimati, “I—ine ndithudi ndimamvera chisoni nkukhu zobalidwira mu makina.” Inu mukudziwa, nkukhu yaing’ono yomwe imabalidwa pansu pa makina, iyo siinabalidwe moyenera. Ayi. Nkukhu imayenera kuti izibala mwanapiye. Koma mwanapiye wa mmakina, pamene iyo itulukamo, iyo basi “piye, piye, piye,” ndipo iyo ilibe amake oti ipiteko. Mukuona? Iyo siimadziwa yemwe ali mayi wake. Ndiko kulondola. Iyo ikumulirira iye, koma iyo ilibe wina aliyense.

382 Koma mwanapiye wamng’ono yemwe waswedwa pansu pa thazi, mwanjira yachirengedwe, iye amalira ndipo make amayankha. Ndiko kulondola.

383 Ndipo nthawizina ine ndimaganiza zokuchitikirani za ku seminare izi kuno zochokera pansu pa zoutamira zazikulu izi mu Louisville ndi mdziko lonse, kuswa azilaliki natuluka mwa zikwi. Zoutamira za Chipentekoste, ndi zoutamira za Apresbateria, n—ndi zoutamira za Chibaptisti, izo zonse zimaswa ndi kutulutsa a—a—anapiye awo aang’ono. Izo, “zimalira, piye, piye,” ndi kumayankhula za choutamirira chomwe izo zinaswedweramo.

384 Koma ine ndimakonda kukhala ndi Atate, Amayi. Lodala likhale Dzina la Ambuye! Sanali ochuluka kwambiri anabadwa ndi ine, koma omwe analipowo anali abale anga. Ameni. Ife tiri nawo Amayi omwe amayankha pamene iwe. . . Mayi yemwe ali Kumwamba, yemwe anachita Umayi pa ife tonse. “Monga thazi liwutamira pa anapiye ake, ndi kumayimba kwa iwo, n—ndi kukopa pa iwo. . . kufungatira pa anapiye ake, chomwechonso ine ndizifungatira pa inu. O, Yerusalemu, Yerusalemu, ndi mowirikiza chotani ine ndikanati ndikutenge iwe monga nkuku imachitira ana ake! Ndi kangati ine ndikanati ndikupangeni inu kukhala Anga, koma inu simukufuna. Inu munali ndi maseminare anu anu, mumaswa ansembe anu natuluka. Iwo anakuphunzitsani inu motsutsana ndi Ine. Tsopano inu mwasiyidwa panokha. Chiwonongeko chanu chiru patogolo panupo.”

385 Ine ndikunena izi. O, anthu! O, anthu, ndi kangati Mzimu Woyera ukanati ukufungatireni inu, monga nkuku imachitira anapiye ake! Koma inu mukufuna njira yanu yanu. Inu mukuti mukhale ndi njira yanu yanu ya Iwo.

386 Limodzi la mausiku awa ine ndikanafuna kuti ndidzalalikire pa, “Njira yanu yanu.” Inu mukudziwa, Kaini ankafuna njira yake yake. Munthu amafuna njira yake yake, lero. “Koma pali njira yomwe imawoneka ngati yabwino, koma mapeto ake ndiwo imfa.”

387 Tsopano penyani. “Mwakuti Iye anati, ‘Latsopano—pangano latsopano. . .’” Ine ndikukhulupirira, tsopano apo. . . Ayi. Ine ndinali pa malo olakwika.

388 Ndime ya 28.

Pakuti lamulo limawapangitsa amuna kukhala ansembe aakulu omwe ali ndi zifooko; koma mawu a lumbiro, omwe anali chiyambireni lamulo, amamupanga Mwana, yemwe ali mopitirira kwanthawizonse mochulukuka.

389 Mulungu akhale wodalitsidwa kwanthawizonse, wa Mwana yemwe akupitirira kwanthawizonse motsatira dongosolo la Melkizedeki. Ndipo Iye analibe konse chiyambi. Iye alibe konse mapeto. Ndipo lamulo silikanapereka chinthu china chonga chimenecho, chifukwa ilo linali lachithupithupi. Mpingo sungakhoze kupereka chinthu china chonga chimenecho,

zipembedzo, chifukwa izo ndi zachithupithupi. M—maseminare sangakhoze konse kubala chirichonse chonga chimenecho. Iwo anayesera kuliphunzitsira dziko kwa Iwo. Iwo anayesera kupangira bungwe kwa Iwo. Iwo ayesera njira iliyonse mu dziko, kuti apange chirichonse chomwe iwo akanakhoza, ndi kusiya pambali chinthu chenichenicho: “Inu mumayenera kuti mubadwire Mmenemo.” Mulungu amakupangani inu chomwe inu muli, ndithudi, osati chifukwa inu mwasiya kuchita *izi*.

³⁹⁰ Tsopano, Anazerini, inu mumachita kusiya kuvala mphete, inu simungati muvale wotchi, ndipo inu mumayenera kuti muzikhala ndi zinthu *zakuti-zakuti* zinazake, mikono yanu iyenera kuti izitalika *chotere*, mikono ya malaya, masiketi anu azitalika *chotere*, n—ndipo amuna asamakhale a mu chigono. Ndipo iwo sangati akubatizeni inu ngati inu simutero. Chabwino. Apa pakubwera a Chikatolika, ndipo iwo ali nazo zawo. Ndipo apa pakubwera Achimethodisti, iwo ali nazo zawo. Aliyense wa iwo ali ndi muyezo woyezera kuti ufikepo. Inu mukapanda kukwaniritsa izo, chabwino, zathera pomwepo. Mwaona?

³⁹¹ Ndiyeno, koma chinthu chenicheni ndicho, ndi ichi, “Palibe kanthu mmanja mwanga ine ndikukabweretsa! Mophweka ku mtanda Wanu ine ndikukangamira. O Mulungu, wamaliseche, wovulazidwa, wosowa kuyamwa. O, ine modzichepetsa kwambiri ndikubwera, Khristu, kuvomereza kuti sindine kanthu ndipo mulibe kalikonse mkati mwa ine. Ndilandireni ine, O Mulungu.” Ndiye Mulungu amakulandirani inu.

³⁹² Tsopano, inu mukhoza kusamadziwa nkomwe ABC wanu. Inu mukhoza kusamadziwa khofi kwa nyemba zobanthulidwa. Inu mukhoza kudziwa, osadziwa gii kwa hoo, dzanja lamanja kwa lamanzere. Izo sizimapangitsa kusiyana kulikonse chomwe inu simumachidziwa. Pali chinthu chimodzi chomwe inu *muyenera* kumachidziwa, kuti, Yesu Khristu anatenga malo anu ngati wochimwa. Ndipo inu mutenge malo anu, kuti muziima mu chilungamo Chake, kuvomereza tsiku lililonse kuti ndinu olakwa, ndi kumamukonda Iye ndi mtima wanu wonse, ndi zokupangitsani zanu zonse zikhale zokhazikitsidwa kwa Iye, inu mudzakafika Kumwamba. Ndizo zonse zomwe ziripo kwa izo, pakuti Moyo umene unali mwa Khristu uyenera kuti ukhale mwa inu, kapena inu mwataika.

³⁹³ Basi tisanati titseke, kodi inu mukukumbukira pangano lopanda mangawa lomwe Mulungu anapanga ndi Abrahamu? Kodi Iye anachita chiani usiku uja pamene Mulungu anati, “Ndiroleni ine ndiwone...” Pamene Abrahamu anati, “Ndiroleni ine ndiwone momwe Inu muti muchitire izo.” Mutu wa 16, ine ndikuganiza apo pali, wa Genesis. “Ndiroleni ine ndiwone momwe Inu muti muchitire izo.”

394 Anati, “Bwera kuno, Abrahamu.” Ndipo Iye anamuchotsapo Abrahamu, anati, “Pita ukanditengere ine—nkhosa, ndipo pita ukanditengere ine—m—mbuzi, ndipo pita ukanditengere ine ng’ombe. Ndipo ine ndikufuna kuti iwe uzitengere izo pamwamba pano ndi kupanga nsembe.”

395 Ndipo Abrahamu anapita ndipo anakatenga nkhosa, n—ndi mbuzi, ndi—m—mwanawankhosa . . . kapena ng’ombe. Ndipo iye anazipha izo. Izo zonse zinali nsembe zoyera. Ndipo anazidula izo pakati mzibanthu ziwiri, ndipo anaziyala izo apo. Ndiye iye anapita ndipo anakatenga nkhunda ziwiri, ndipo anaziponyera izo umo. Ndiye Abrahamu ankayang’anira mbalame kuti zisafike pa izo, akuyembekezera kuti Mulungu abwere. “Tsopano, Ambuye, ndi iyo nsembeyo, Inu muchita motani izi? Ine sindikudziwa momwe Inu muti mumupulumutsire munthu motsutsana ndi chifuniro chake chomwe. Ine sindikudziwa momwe Inu muti muchitire izi. Inu mungachite motani izo, Ambuye?”

396 Ambuye anati, “Tsopano penya, Abrahamu. Ndiwe mneneri. Ndiwe wauzimu, ndipo iwe umvetsa zomwe ine ndikuzikamba.”

397 “Chabwino, Ambuye, ine ndikufuna kuti ndiwone.” Tsopano ine ndikungochita mwasewero.

398 “Kotero, Abrahamu, iwe bwera pano tsopano, ndi kukhala pansu apa ndi kumayang’anira mbalame izo pano zisamafikepo.” Kotero iye ankazithamangitsa mbalame zonse zichokepo, mpaka dzuwa linayamba kulowa.

399 Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, Mulungu anabwera pansu. Pamene Iye anabwera pansu, Abrahamu anayamba kukhala watulo. Mulungu anati, “Abrahamu, ine ndikuti ndikugonetse iwe tulo.”

400 Tsopano mvetsera, mzanga wamwalamulo. Mukuona, Mulungu anamuchotsa Abrahamu kwathunthu pa chithunzipo, palibe kalikonse nkomwe iye akanati achite mu icho. Ndipo umo ndi momwe Iye anakutengerani inu. Inu mumati, “O, ine ndinafunafuna Mulungu.” Inu simunatero.

401 Mulungu anakufunanifunani inu, “Palibe munthu angadze kwa Ine kupatula Atate Anga atamukoka iye poyamba.” Mukuona?

402 Ndi Mulungu kukufunanifunani inu, osati inuyo kumufunafuna Mulungu. Inu simunachitepo konse izo. Chibadwa chanu ndi cholakwika. Ndinu nkhumba. Inu simumadziwa kusiyana kulikonse. Inu mumangokhala mu khola la nkhumba. Ndizo zonse zomwe inu mumazidziwa. Inu mumazikonda izo. Kumwa mowa, kulowerera apa, kuthamanga ndi mkazi wa mwamuna wina, ndi kumachita chirichonse chimene inu mungakhoze kuchita chiri choipa, basi zimangowoneka zabwino. “O, m’bale, ife tikumakhala ndi nthawi yaikulu!” Inu mumaganiza kuti ndi zabwino.

403 Koma Mulungu amagogoda pa mtima wanu. [M'bale Branham akugogoda pa guwa—Mkonzi.] Ndi zomwe zimakusinthu. Osati inu kugogoda kwa Mulungu; Mulungu amagogoda pa inu. Adamu sanagogode konse ku mtima wa Mulungu. Mulungu anagogoda pa mtima wa Adamu. Ndipo inu ndinu mwana wa Adamu. Ndiko kulondola. Adamu asanati konse akhale mwana wa Mulungu, kachiwiri, Mulungu anagogoda pa mtima wake. Inu musanati mukhale mwana wa Mulungu, Mulungu amayenera kuti agogode pa mtima wanu.

404 Ndiye, Abrahamu anagona tulo. Ndipo pamene iye anagona tulo, chinali chiani chinthu choyamba chimene iye anachiwona? Wowopsya kwenikweni, wazipukupuku, mdima wowopsya. Ndiyo imfa, yomwe imabwera pa mtundu wonse wa anthu. Ndiye iye anayang'ana patsogolo pang'ono kuposa apo, ndipo iye anawona ng'anjo yofuka. Inu musanakhale ndi utsi, inu mumayenera kukhala ndi moto. Ndi chifukwa chake ine ndimakhulupirira kuti kuli gehena monga malo oyaka. Chabwino.

405 Iye ankasonyeza kuti, aliyense wa ife ali woti adzafa, ndipo aliyense wa ife anayenera kupita ku gehena, chifukwa ndife ochimwa.

406 Tsopano, koma, kupitirira izo, iye anawona Kuwala kwakung'ono, koyera.

407 Ndipo Kuwala kwakung'ono, koyera uku, kodi Kuwala ndi chiani? Kuwala koyera kuja kunali chiani? Lawi la Moto lomwe linkapita patsogolo pa ana a Israeli. Lawi la Moto limene linakomana naye Paulo pa njira yaku Damasiko. Lawi la Moto limene linamutenga Petro kumchotsa mu ndende. Lawi la Moto lomwe liri pano usikuuno.

408 Mulungu Wamuyaya, wosatha uja, Iye Mwiniwake anayenda pakati pa nsembe zogawanizidwa izi, (o, mai), mmbuyo ndi mtsogolo pa ina iliyonse. “Umu ndi momwe ine nditi ndichitire izo, Abrahamu. Ndipenye Ine, zomwe ine nditi ndichite. Ine ndikupanga pangano apa. Ndipo ine nditenga lumbiro, kuti, malingana ndi Mbewu, ine ndidzutsa Woyimira pakati. Ine ndipanga pangano ndi imfa. Ndipo ine ndiiweruza imfa, mu thupi, chifukwa Ine Mwini ndibwera kudzaitenga iyo. Abrahamu,” anati, “kupyolera mu Mbewu yako, Abrahamu, adzabwera. Iwe udzakhala tate wa dziko lonse, kupyolera mu Mbewu yako. Ndipo si iwe wekha, kuti ine ndipanga lonjezo ili ndi iwe, koma Mbewu yako ya pambuyo pako.” Iye ankadziwa kuti aliyense akanadzakhala. “Osati *iwu*; koma chimene ine ndichita. Ine ndikuti ndichite izo, Abrahamu. Ine ndinadalira Adamu, ndipo iye anaswa lake. Ndipo aliyense akuswa awo. Koma ine ndipanga ili ndi Inemwini, ndipo ndilumbira pa Inemwini, ‘Ine ndilisunga Ilo.’” Ameni. Ameni. Ameni.

409 Kodi ife timachita chiani, kuti ife tipange pangano? Ine ndingati, “M’bale Neville...” Tsopano penyani ichi, miniti yokha. Ine nditi, “M’bale Neville, ndikuuzeni inu chimene ine nditi ndichichite. Ngati inu muti mulalikire mpaka...mawa usiku, ndi usiku wotsatira, mpaka Lachitatu. Ine ndidzalalikira, kuyambira Lachitatu, mpaka Lamlungu.” [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] “Inu mupanga chigwirizano chimenecho?”

410 “Inde, bwana.”

411 Apa pali njira yomwe ife timachitira izo. “Ndigwire chanza, mnyamata.” [M’bale Branham ndi M’bale Neville akugwirana chanza—Mkonzi.] Ndi zomwezo. Ndilo pangano mu Amereka. Ndi momwe ife timapangira pangano.

412 Tsopano, amapanga bwanji pangano mu Japan? Ife timapanga, timati, “Iwe ukachita *chakuti-n-chakuti*, ndipo ine ndichita *chakuti-n-chakuti*. Ife titenga mchere pang’ono, chifukwa mchere ndi wotetezera. Ndipo ife titenga mchere, ndipo ine nkuuponyera iwo pa M’bale Neville, ndipo M’bale Neville natenga mchere—mchere ndi kuwuponyera iwo pa ine. Limenelo ndi pangano lomangiriza.

413 Kodi David Livingstone anapanga motani pangano ndi wachikuda waku Afrika, kuti apite mu dziko lake? Iye anapita ndipo amakamutenga mfumu, kuti iye akhoze kudutsa kumeneko, kuti azikalalikira Uthenga ndi kukachita ntchito yawo. Ndipo iwo anatenga chikho cha vinyo. Ndi limeneli pangano ndi wachikuda waku Afrika. Iwo anatenga chikho cha vinyo. Ndipo mfumu yachikuda inadula misempha yake yomwe, ndipo inakhetsera iyo mu chikho cha vinyo ichi. Ndipo David Livingstone anadula misempha yake yomwe, ndipo anaikhetsera mu chikho cha vinyo. Iwo anazisakaniza izo. Livingstone anamwa theka la izo, ndipo mfumu yachikuda inamwa theka la izo. Ndiye iwo anapatsana mphatso, wina kwa mzake, mfumu yachikuda. David Livingstone anati, “Inu mukufuna chiani kwa ine.”

414 Iye amati, “Chikhoto choyera icho chomwe inu mwachivala.” Chotero Livingstone anavula chikhoto chake ndipo anachipereka icho kwa mfumu yachikuda. Iyo inati, “Kodi inu mukufuna chiani?”

415 Iye anati, “Nkondo wopatulika uwo womwe inu muli nawo mu dzanja lanu.” Chifukwa, iye ankadziwa kuti iye akanakhoza kulowa umo ndi umenewo, chotero iye anatenga nkondo umenewo. Ndipo iwo anali abale, chifukwa iwo anapanga pangano.

416 Ndipo pamene iye anali kupita uko, ndipo mafuko ankakhoza kuthamanga kuti adzamuphe iye, iye ankakwezera mmwamba nkondo wopatulika uwo. Ndipo pamene iye ankatero, iwo ankayang’ana ndipo ankati, “O, o, ife sitingakhoze kumukhudza munthu ameneyo.” Bwanji? “Iye ndi m’bale

wapangano, ngakhale iye ali mzungu, ife sitinayambe tamuwonapo iye kale.” Iwo sankadziwa kuti iwo anali akuda mpaka iwo atamuwona iye. Iwo anali asanayambe awonapo choterocho kale. “Koma iye ndi m’bale wapangano. Iye ali ndi nkondo wa a mfumu mu dzanja lake.”

⁴¹⁷ Ndi chithunzi chokongola bwanji, lero, cha kumwa pangano la Magazi a Ambuye Yesu, ndi mphamvu ya Mzimu Woyera ili pa ife! Ife timapita mtsogolo mu Dzina la Yesu, ndipo zizindikiro izi zidzawatsatira iwo omwe ali ake. Iwo ndi Nkondo wopatulika wa Mfumu. Mukuona momwe ilo liriri, pangano?

⁴¹⁸ Kodi ankachita chotani izo mu nthawi yamakedzana? Iwo ankapanga lumbiro, wina kwa mzake. Iwo ankapha chinyama, ankachitsegula icho mzibanthu, ndipo ankaima pakati pake pomwe. A—amuna awiriwo ankaima pakati pa iyo, nyama yobanthulidwayo. Ndipo iwo ankalilemba pangano. “Ngati ine nditi ndilephere kusunga *ili*, ngati ine nditi ndilephere kuchita *izi*, bwanji, *izi* ndi *zakuti-n-zakuti*, mudzalole thupi langa lidzakhale ngati chinyama chakufa ichi. Mudzalole thupi langa lidzakhale ngati chinyama chakufa ichi.” Ndipo pamene iwo achita izo, iwo ankatenga pangano ili ndi kuima pakati pa *izi*; ndipo ankapanga lumbiro, ankapanga lumbiro kuti iwo achita izo. Ndipo iwo ankang’ambirana chi pepalacho, palimodzi, ziduswa, ndi kupereka ilo kwa munthu mmodzi, winayo lotsatiralo. Pa nthawiina iwo adzakomana. Ndipo iwo adzaloledwe kufa imfa, ngati iwo alephera kusunga lumbiro limenelo; ndi kukhala monga zinyama zakufa zija. Chabwino.

⁴¹⁹ Inu mukuzindikira zinyama zitatu? Zangwiwo; mwanawankhosa, mbuzi...ndi nsembe zitatu zangwiwo. Kodi mwanawankhosa anali chiani...Kodi nkhunda inali chiani? Ndipo kodi nkhunda ziwirizo zinkatanthauza chiani? Nkhunda ziwirizo zinali kuperekedwa nsembe kwa zonse chipulumutso ndi machiritso, m—mu...zomwe zinkapita mu ilo. Mukuona? Chitetezero chinali kupangidwa, mosiyana, koma machiritso anapitirira chimodzimidzi, ndi momwenso chipulumutso chikupitirira chimodzimidzi. Nkhunda ziwiri, zosagawanizidwa, zinkatanthauza apo zinkaimirira, zonsezo. Chipulumutso... “Ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa. Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu. Ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Izo zinkaikidwa pa mbali, osati kulekanitsidwa. Koma pangano, gawo la nyama (zitatu za izo) zinkadulidwa mzibanthu. Inu mukuona? Ndiye pamene iwo ankachita izo, iwo ankang’amba ndipo ankapanga pangano lawo.

⁴²⁰ Penyani zomwe Mulungu anali kumuza Abrahamu. “Pa Kalvare, pa Kalvare, malingana ndi Mbewu yako. Kuchokera mwa iwe munatuluka Isaki. Kuchokera mwa Isaki munabwera *wakuti-n-wakuti*, Yakobo. Kuchokera mwa Yakobo munabwera Yosefe. Kuchokera mwa Yosefe, mpaka pansi, mpaka pansi,

mpaka pansi, olowammalo, mpaka, potsiriza, kupyolera mu Mbewu yolungama iyo!” Yake. . .

⁴²¹ Iye watsiriza kumene, apa, kunena kuti Ambuye wathu anatuluka kuchokera mu fuko lomwe silinkamudziwa Mose, sankayankhula ngakhale za izo. Anabwera kuchokera mu unsembe. “Ambuye wathu anaphukira kuchokera ku fuko la Yuda.” Osati kuchokera kwa Levi, pakuti iwo anali amwalamulo achithupithupi. Koma Ambuye wathu anabwera kuchokera kwa Yuda. Ulemerero! Ndi inu apo. Komwe lonjezo linapangidwa!

⁴²² Mvetserani mwacheru tsopano, pamene ife tikutseka. Ndipo pa Kalvare, Mulungu anabwera pansi ndipo anatenga thupi la Mwana Wake yemwe, momwe Iye anali atakhalamo, ndipo Iye analikhadzula ilo mmabanthu pa Kalvare. Kuwukha magazi Kwake, atavulazidwa, atadulidwa, ndi nthungo itapyoza mmenemo ndipo anamukhadzula Iye mzibanthu, ndipo Magazi Ake anakhavukira panja. Ndipo Iye anati, “Atate, mmanja Mwanu ine ndikuwupereka Mzimu Wanga.” Iye anaweramitsa mutu Wake. Ndipo dziko lapansi linagwedezeka, ndipo mphezi zinang’anima, ndi mabingu anabangula. Mulungu anali akulemba pangano Lake losatha.

⁴²³ Ndipo Iye analitenga thupi Lake lakufa kuchokera mmanda, pa tsiku loyamba la sabata, ndipo analibweretsa ilo Kumwamba, ndipo anadzalikhazika ilo pamenepo monga Wansembe Wamkulu, ngati chikumbutso; atakhala pamenepo, wangwiro, kwanthawizonse. Ndipo Iye anatumiza Mzimu womwe Iye anaung’amba nachotsa mu thupi lija, kuti ubwerere kumene pa Mpingo. Ndipo Mpingo uwo uyenera kuti ukhale ndi Mzimu womwewo umene unali mu thupi limenelo, kapena ilo silidzalumikizana bwinobwino ndi Ilo mu chiukitsiro. Zibanthu ziwiri izo ziyenera kubwera mwangwiro palimodzi. Ndipo ngati Mpingo uwo sululi mwangwiro, ndendende basi Mzimu womwewo umene unali mwa Khristu, inu simudzapita konse mu Mkwatulo.

⁴²⁴ Ndi limenelo pangano losatha, m’bale. Lifuneni ilo, mwiniwanu, chomwe chiri mu mtima wanu momwe. Ziwakondani Ambuye. Khalani wotsimikiza kwenikweni kuti inu munapulumsidwa. Musati mutengere mwayi pa izo. Inu mukuchita wachionandani. O, inu, ife anthu Achimereka, timakonda kuchita wachionandani, koma musati muchite wachionandani pa Zimenezo. Inu mukhale otsimikiza kuti inu mukulondola. Osati chifukwa kuti inu munalowa mpingo, koma chifukwa kuti inu muli moona obadwa kachiwiri, Khristu wabwera kwa inu, mwa Umunthu wa Mzimu Woyera.

⁴²⁵ Tsopano, mongowonjezera, aponso, basi pamene ine ndikutseka. Momwe ife tiyenera kumakhalira okondwa, powuwona Mzimu womwewo umene unali mwa Yesu Khristu, uli pakati pathu pomwe, ukuchita zinthu zomwezo zimene Iye

ankachita pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi! Momwe ife tiyenera kumakhalira okondwa!

Tiyeni ife tipemphere tsopano, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu.

⁴²⁶ Ambuye, ili lakhala liri tsiku lalikulu. Ngakhale, ine ndimamverera monga ine nthawizonse ndimachitira, ine ndimalephera. Ine sindingakhoze kuziimira Izo molondola, Ambuye. Ine ndikupemphera kuti Inu mundikhululukire ine njira zanga zopusa. O, ine ndikuvomereza machimo anga pamaso pa Inu, ndi kupempha chifundo, podziwa kuti pali Wansembe Wamkulu akuima kutaliko ku dzanja lamanja la Mulungu, mu Miyamba, yemwe sanapangidwe motsatira Aroni, motsatira malamulo ndi zovomerezeka ndi zinthu. Koma Iye anaikidwa Pamenepo chifukwa cha chisomo cha Mulungu chimene chinkayang'ana kutsogolo, asanaikidwe maziko a dziko, ndipo anandiwona ine pansi pano mu dziko, ndipo anafera machimo anga, kuti andibwezeretse ine ku Ufumu wa Mulungu. Ine ndikukuthokozani Inu, Atate, chifukwa cha izi.

⁴²⁷ Chifukwa, Mzimu uwu umene tsopano ukulamulira mwa anthu anu uli Wamuyaya monga Mulungu ali Wamuyaya. “Ine ndimapereka kwa iwo Moyo Wamuyaya, Moyo wanthawizonse, Moyo wosatha, ndipo iwo sadzaonongeka konse.” Ndipo pa Chiweruzo, iwo sadzakhala konse uko. Iwo anadutsa kale ziweruzo ndipo anapita mpaka mu Ulemerero, “Ndipo ngati msasa wapansi uno usungunuka, ife tiri nawo wina kale ukuti yembekezera kutsidyako kuti ife tibwere kwa iwo.” Zikomo Inu chifukwa cha izo, Ambuye.

⁴²⁸ Ine ndikupemphera tsopano, ngati pangakhale wina pano, usikuuno, yemwe sanamwe konse panobe Magazi enieni a pangano, yemwe sakudziwa chomwe Iwo amatanthauza, sakudziwa chomwe chimatanthauza kukhala utabadwa kachiwiri, kukhala nacho chiyanjano chenicheni ndi Khristu mu mtima mwawo, kapena mtima wake, mulole iwo amulandire Iye pomwe pano, pamene ife tikudikirira ndi kupereka mwayi uwu. Ndipo pa Tsiku limenelo, ife tikupemphera kuti ife tidzakhale titaumira Uthenga mu Kuwala kolondola. Ife tikupemphera, mu Dzina la Khristu.

⁴²⁹ Pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa, kodi pangakhale munthu yemwe mungakweze manja anu kwa Khristu, ndi kuti, “Khristu wa Mulungu, khalani achifundo kwa ine. Mundirole ine, monga wantchito Wanu wosayenera, tsopano ndilandire Mzimu Woyera mu mtima mwanga. Ndipo ndipatseni ine chitsimikiziro ndi chikondi zomwe ine ndikuzisowa kwenikweni”? Ngati inu mulibe Iwo, kodi inu mungangokweza manja anu kwa Iye, ndi kuti, “Ambuye, ichi ndi chisonyezo kuti ine ndikuwukhumba Iwo”? Kodi inu mungaike dzanja lanu mmwamba? Mulungu akudalitseni inu kumbuyo uko, dona.

Mulungu akudalitseni inu apa, bwana. Akudalitseni inu apa, bwana. Mulungu akhale ndi inu. Izo ndi zabwino. Bambo uyu pa mapeto apa, Mulungu akudalitseni inu, m'bale wanga. Ndi wina wakenso, basi tsopano ife tisanatseke, tikungoyembekezera kwa mphindi pang'ono. Mulungu akudalitse iwe kumbuyo uko, mwananga. Wina wakenso?

⁴³⁰ Ine tsopano ndikukhumba. Ine ndikukhumba, Ambuye Mulungu. Inu mukuwudziwa mtima wanga. Inu mukudziwa chimene chiri mu malingaliro anga. Inu, 'Mzimu wa Mulungu uli wachangu ndi wakuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, opyoza ngakhale mpaka mu mafuta a mu fupa, ndi ozindikira malingaliro a mu mtima.'" Taganizani za Zimenezo. Iye akudziwa malingaliro anu omwe, zolinga zanu.

⁴³¹ Kodi inu mungakweze dzanja lanu, ndi kuti, "Khalani achifundo kwa ine, Mulungu, pakali pano. I—ine ndikufuna Inu mudziwe kuti ine ndikudziwa kuti ine ndikulakwitsa, ndipo ine ndikuzindikira izo, koma ine ndikufuna ndikhale wolondola." Chabwino, pamene ife tangosiya mitu yathu chowerama, popemphera tsopano, ganizani mphindi yokha. Ife sitikufuna kufulumira pa izo.

Thanthwe la Mibadwo, ndiphimbeni,
Ndibisale mwa Inu;
Mlole madzi ndi Magazi,
Zochokera mmbali Mwanu . . .
Zikhale kwa tchimo kaw- . . .

Machiritso apawiri! Iye analumbira pa izo, zinthu ziwiri zosasintha.

Zichotse mkwiyo nkhale wangwiro.
Pamene ndiyandikira . . .

⁴³² O Ambuye, perekani pakali pano kuti ife tonse tizindikire kuti mpweya uwu umene ife tikuukokawu ukutha. Ife sitikudziwa kangati kenanso komwe tiri nawo mtsogolo mwathu. Zonsezo ziri za mwa uphungu Wanu wawukulu. Izo ndi zokonzedwa ndi Inu. O, khalani achifundo kwa ife. Ndipo kwa iwo omwe anakweza manja awo, Ambuye, palibe kusowa koti ndiwatchulire iwo. Inu mukuwadziwa aliyense wa iwo. Koma ine ndikungopereka pemphero ili la kuimira pakati kwa iwo. Ine ndikupemphera kuti Inu muchotse kutsutsidwa mu mtima mwawo, ndi kuwalola iwo abwere molimba mtima, pakali pano, ku Mpandowachifumu; ayende molimba mtima mpaka ku Mpandowachifumu wa Mulungu, adzatenge za mwayi wawo wopatsidwa ndi Mulungu. Inu munawapangitsa iwo kuti akweze manja awo. Iwo sakanati achite izo mwa iwoeni. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu mupereke izi mu Dzina la Yesu. Amen.

. . . ine mwa Inu;

Tsopano, zingomamupembedzani Iye tsopano.

Mlole madzi ndi . . . (O, mai!)
 Zochokera mmwali Mwanu,
 Zichize tchimo pawiri,
 Zichotse mkwiyo n'khale wangwiro.

433 Ndi angati akumverera bwino kwenikweni
 tsopano? Kwezani mmwamba dzanja lanu, ndi kuti,
 “Ambuye Alemekizeke!” [Osonkhana ati, “Ambuye
 alemekizeke!”—Mkonzi.] O, Iye ndi wodabwitsa! O!

Pali Malo Pa Kasupe. Kodi inu mukuidziwa iyo, Mlango
 Gertie? Tiyeni. Ndi angati amaikonda nyimbo imeneyo? Tsopano
 ife tikhala ndi utumiki wa ubatizo, mu mphindi chabe.
 [M'bale Branham akuyankhula ndi M'bale Neville—Mkonzi.] Inu
 muwabatiza iwo? Chabwino.

Malo, eee, pali malo,
 Pali malo anu pa Kasupe;
 Malo, malo . . .

434 Chabwino. Oyenera kuti abatizidwe aja, amuna apita ku
 chipinda *ichi*, akazi ku *ichi*, chabwino, awo oti abatizidwe mu
 Dzina lodala la Ambuye wathu.

. . . abwino kwa inu,
 Pali malo anu pa Kasupe;
 Mulungu wakhala wabwino kwa ine,
 Pali malo anu pa Kasupe.

435 Aliyense tsopano.

Malo, malo, eee, pali malo,
 Pali malo anu pa Kasupe;
 Malo, malo, eee, pali malo,
 Pali malo anu pa Kasupe.

436 O, ine ndimaikonda nyimbo yachikale iyo. Sichoncho inu?

Pali malo anu pa Kasupe;
 O, malo, malo, pali malo ambiri,
 Pali malo pa Kasupe.

437 Tsopano, pamene aakulu alowa umo, kuti akakonzekere
 ubatizo, ine ndikufuna kuti ndilongosole kwa omvetsera.
 Ndipo ine ndikanapempha ena a madikoni, ngati iwo akukhoza
 kundimva ine mu chipindamo, pamene iwo akonzeka, abwere
 n—ndi kudzandiuza ine, ndipo chotero ife tithe kusuntha
 zoyankhuliramo. Ife timafuna kuti nonse inu muziwona
 izi. Zikhala pafupi miniti khumi motalikira, ndipo mpingo
 ubalalitsidwa.

438 Tsopano ine ndikufuna kuti ndiwerenge ena a Malemba
 opatulika kwa inu. Ine ndikufuna kuti ndiawerenge iwo
 kuchokera mu Bukhu la Machitidwe. Ndipo ine ndikufuna kuti
 ndiyambire pa ndime ya 12 ya mutu wa 2 wa Machitidwe.

439 Tsopano, ine ndikufuna kuti inu muzindikire mu mutu wa 16 wa Luka Woyera, kapena Mateyu Woyera, ine ndikukhulupirira iwo uli, pamene Yesu anali kubwera kuchokera mphiri. Iwo. . . Ananena kwa ophunzira Ake, “Kodi anthu amati ine Mwana wa munthu ndine yani?”

440 “Ndipo ena a iwo anati, pakuti, Ndinu ‘Eliya.’ Ndipo ena amati Ndinu—ndinu ‘mneneri.’ Ndipo ena amati Ndinu *uyu* kapena *winayo*.”

441 Iye anati, “Koma ndi yani yemwe inu mukuti Ine ndiri?”

442 Ndipo Petro anati, “Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo.” Nkulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

443 Yesu anati, “Wodala uli iwe, Simoni Mwana wa Yona, pakuti thupi ndi mwazi sizinakuululire izi. Iwe sunaziphunzire izi konse mu seminare. Iwe sunaziphunzire izo ndi munthu.” Anati, “Koma Atate anga omwe ali Kumwamba awululira izi kwa iwe. Ndipo ine ndikuti iwe ndiwe Petro. Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga. Zipata za gehena sizidzawulaka Iwo. Ndipo ine ndipereka kwa iwe mafungulo aku Ufumu wa Kumwamba.” Ndi kulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] “Ndipo chirichonse chomwe iwe uchimasula padziko lapansi, Ine ndichimasula icho Kumwamba. Chimene iwe uchimanga padziko lapansi, Ine ndichimanga Kumwamba.” Kodi Iye ankatanthauzadi Zimenezo? Iye sakanati anene Izo. Tsopano, pamene nthawi inapitirira—pitirira mtsogolo, tsopano. Petro anali ndi mafungulo a ku Ufumu.

444 Tsopano, inu anthu Achikatolika, inu mukhoza kuganiza izi, kuti inu mumati, “Mpingo wa Katolika unamangidwira pa Petro.” Chabwino, ife tizifufuza. “Iwo anali ndi mafungulo. Mpingo wa Katolika ukadali nawo mafungulo.”

445 Tiyeni tifufuze zomwe *Petro* anachita nawo mafungulowo, onani, ndiye ife tizipeza. Baibulo linati, kwa Petro ndi kwa ophunzira enawo, “Pitani inu ku dziko lonse. Machimo a aliyense omwe inu muwachotsa, kwa amenewo iwo achotsedwa. Machimo a aliyense omwe inu muwasunga, kwa amenewo iwo asungidwa.” Kutu, Ine ndikhoze kunena izo kuti. . . Mwina wina angalephere kumvetsa zomwe ine ndikutanthauza. Yesu anati kwa ophunzira, “Machimo a aliyense omwe inu muwakhululukira, ine ndiwakhululukira iwo aponso. Ndipo machimo a aliyense omwe inu simuti muwakhulukire, ndi kuwasunga iwo mowatsutsa iwo, Ine ndiziwasunga iwo mowatsutsa amenewo aponso.” Ndi zomwe Yesu ananena.

446 Penyani mpingo wa Katolika ukusunthira cha kwa izo.

447 Koma tiyeni tifufuze momwe iwo ankachitira izo. Ndiye ngati titi tipeze momwe iwo ankachitira izo, ndiye ife tiyenera kumachita izo mwanjira yomweyo. Tsopano tiyeni tifufuze.

448 Ndi Tsiku la Pentekoste. Mpingo uli nkutseguliridwa. Iwo onse anali mu chipinda chammwamba. Amuna anatuluka kuchokera umu, akuyankhula mu zinenero zosiyana. Bwanji? Chinenero chirichonse cha pansu pa Kumwamba chinaimiridwa kumeneko. Chingerezi chinali kumeneko, nachonso. Chinenero chirichonse cha pansu pa Kumwamba chinkayenera kukhala chiri kumeneko, chinenero chimene chinkayankhulidwa mu tsiku limenelo. Akupitirira apa ndi kupereka zambiri za zinenerozo, ndi momwe Akurete ndi alendo, ndi otembenezidwa aku Roma, n—ndi Aruya, ndi onse akuyankhula ndi unyi-... Tsopano, iwo sanali kuyankhula mu malirime osadziwika. Iwo anali akuyankhula mu zinenero zodziwika, kwa anthu. Osati malirime osadziwika, koma zinenero zomwe aliyense ankazimva. Wochimwa, wosakhulupirira, ankakhoza kumva zomwe iye anali kunena. “Ife tiri kumva bwanji mu chinenero chatu chomwe cha k—komwe ife tinabadwira?”

449 Tsopano penyani. Tsopano funso likubwera. Tsopano, “Ena ankatonza.” Ndime ya 12, chabwino.

*Ndipo iwo onse anali ozizwa, ndi. . . mwa kukaikira,
nanena wina kwa mzake, kodi izi zikutanthauza chiani?*

*Ena ankatonza ndipo ankati, Awa. . . akhuta vinyo
watsopano.*

450 Iwo anali kuwaseka iwo. Chifukwa, kodi iwo ankachita motani? Iwo anali kuzandima ngati anthu oledzera, ngati anthu oledzera. Kumayankhula, mosadziwa zomwe iwo anali kunena, koma anali kulalikira kwa osonkhanawo mu zinenero zomwe iwo sanali kuzidziwa, koma osonkhanawo ankazidziwa. Mukuona? Chabwino.

*Ena. . . ankati, Iwo akhuta vinyo watsopano, taonani
momwe iwo akuchitira.*

Ena ankanyoza, kumati, Awa. . . akhuta ndi. . .

“Koma Petro. . .” Samalira, mnyamata! Iwe uli ndi mafungulo.

*Koma Petro, ataima apo limodzi nao khumi ndi
mmodziwo, anakweza mawu ake, ndipo anati kwa
iwo, . . .*

Tsopano, kumbukirani, uku ndi kutsegulira koyamba kwa Mpingo.

*. . . Inu amuna aku Yudea, ndi. . . inu omwe
mumakhala mu Yerusalemu, chikhale ichi chodziwika
kwa inu, ndipo mveterani kwa mawu anga:*

*Pakuti awa si oledzera, momwe inu mukulingalira,
powona kuti ili ndi koma ora lachitatu lokha la tsiku.*

Momwela mowa munali musanatsegulidwe apo. Mukuona?

Koma ichi ndi chija chomwe chinayankhulidwa ndi mneneri Yoeli;

. . . izo zidzafika pochitika mu masiku otsiriza, atero Mulungu, ine ndidzatsanulira Mzimu wanga pa mnofu wonse: pa ana anu aamuna ndi. . . aakazi, ndipo iwo azidzalosera, ndipo anyamata anu azidzawona masomphenya, ndipo achikulire anu azidzalota maloto:

Ndipo pa antchito anga ndi. . . adzakazi anga ine ndidzatsanulirapo mu masiku amenewo cha Mzimu wanga; . . . iwo azidzanenera:

Ndipo ine ndizidzasonyeza zodabwitsa mmwamba umo, ndi zizindikiro pa dziko pansipa; . . .

Tsopano, ndi Petro akulalikira tsopano, yemwe anali nao mafungulo.

. . . magari, . . . moto, . . . nthunzi za utsi:

Dzuwa lizidasandulika mdima, . . . mwezi kukhala magari, tsiku lalikulu ndi lodziwika la Ambuye lisanafike:

Ndipo zidzafika pochitika kuti, aliyense yemwe ati azidzaitanira pa dzina la Ambuye azidzapulumutsidwa.

Inu amuna a Israeli, mverani mawu awa; Yesu waku Nazareti, mwamuna wotsimikiziridwa ndi Mulungu pakati pa inu ndi zozizwitsa ndi zodabwitsa ndi chizindikiro, zomwe iye ankazichita. . . pakati pa inu, . . . inu eni anu. . . mukudziwa:

Kunena za chidzudzulo? Iye anali nao mafungulo, inu mukudziwa. Zikhale. . .

Iye, pokhala ataperekedwa mwa upo wotsimikiza ndi kudziwiratu kwa Mulungu, . . .

Ndi inu apo. Iye akanaperekedwa motani? Chifukwa Mulungu anazikonzeratu izo kuti zidzakhale mwa njira imeneyo. Mukuona? Kudziwiratu kwa Mulungu!

⁴⁵¹ [M'bale akuti, a ubatizo wa madzi, "Akonzeka."—Mkonzi.] Mu mphindi yokha. Awuzeni iwo, angodikira miniti yokha, mpaka ine nditsirize Lembali.

. . . inu munamutenga, mwa manja oyipa, munamupachika ndi kumupha:

Yemwe Mulungu wamuukitsa, ndipo wamasula kuwawa kwa imfa; chifukwa izo sizikanakhala zotheka. . . iye kuti akhale atagwidwa nayo iyo.

Pakuti Davide anayankhula zokhudza iye, ine ndinawawoneratu Ambuye nthawizonse. . . kudzanja langa lamanja, ndipo ine sindidzati ndidzagwedezeka:

Chotero mtima wanga unasangalala, ndipo lirime langa linapangitsidwa kukondwera; kuwonjezera apo . . . thupi langa lidzapuma mwa chiyembekezero:

Chifukwa inu simuti mudzausiye moyo wanga mu hade, ngakhalenso kuti mudzalole Woyera wanu kuti awone chivundi.

Inu mwandipangitsa ine kudziwa ine . . . n—njira zanga, njira zanga za moyo; inu mudzandipangitsa ine kudzaza ndi chisangalalo ndi nkhope yanga.

Amuna ndi abale, ndiloleni ine ndiyankhule momasuka kwa inu za kholo Davide, . . . iye ali zonse wakufa ndi woikidwa, ndipo manda ake ali ndi ife . . . tsiku lino.

Chotero pokhala mneneri, ndi podziwa kuti Mulungu analumbira ndi lumbiriro . . .

Ine ndangotsiriza kumene kulalikira izo.

. . . kuti molingana—molingana ndi zipatso za mziuno mwake, iye akanati . . . molingana ndi mnofu, iye akanati adzamudzutse Khristu kuti akhale pa mpando wake;

Basi zomwe ine ndatsiriza kuzilalikira. Petro amalalikira chinthu chomwecho.

Ndipo pochiwona ichi kale, mneneri anachiwona icho kale, ankayankhula za chiukitsiro cha Khristu, kuti moyo wake sukanati udzasiyidwe mu hade, ngakhalenso mnofu wake kuti udzawone chivundi.

Yesu uyu Mulungu wamuukitsa, chomwe ife tonse tiri mboni.

Chotero pokhala atakwezedwa, ndipo ali kudzanja lamanja . . . pokhala kudzanja lamanja, atakwezedwa kumwamba, atalandiridwa ndi Atate . . . lonjezo la Mzimu Woyera, iye . . . wakhetsa apa izi, zomwe inu mukuziwona ndi kuzimva.

Pakuti Davide sanakwere kupita kumwamba, (mneneri): koma iye ananena iyemwini, AMBUYE anati kwa Ambuye wanga, Khala iwe pa dzanja langa lamanja,

Mpaka ine ndiwapange adani ako kukhala chopondera phazi.

Chotero (mvetserani kwa izi) lolani nyumba yonse ya Israeli idziwe motsimikizika, kuti Mulungu wamupanga Yesu yemweyu, yemwe inu . . . munamupachika, kukhala zonse Ambuye ndi Khristu.

Izo zikuyenera kukhazikitsa icho. Sichoncho izo?

Tsopano pamene iwo anamva izi, ochimwa awo, iwo analasidwa mu mitima yawo, ndipo anati kwa Petro . . . Amuna . . . ndipo Petro ndi . . . enawo . . . ophunzira, Amuna ndi abale, kodi ife tichite chiani?

452 Chabwino. Ndi inu apa. Kodi iye ali ndi chiani? Fungulo, fungulo la ku Ufumu. Ufumuwo uli kuti? Iwo uli mkati mwanu. Nkulondola uko? Mzimu Woyera ndiwo Ufumu wa Mulungu. Ife tikuzidziwa izo. Ife tinabadwira mu Ufumu, monga omumvera ndi nthumwi. Onani. Iye ali nawo mafungulo pa mbali pake. “Kodi iwe uchita nawo chiani iwo?” Iyi ndi nthawi yoyamba yomwe chitseko chinayamba chatsegulidwapo.

453 Tsopano, funso linafunsidwa kwa mlaliki, kwa nthawi yoyamba, iye yemwe anali ndi fungulo. Ine ndikukhulupirira ngati iye akanati, “Imani pa mutu wanu,” izo zikanakhala ziri zovomelezeka.

454 “Chirichonse chomwe iwe umanga pa dziko lapansi, ine ndichimanga Kumwamba.” Chabwino. “Chirichonse chimene iwe uchinena, Ine ndinena chinthu chomwecho. Iwe uli nawo mafungulo.” Chabwino. Iye akulowetsa fungulolo pa chitseko.

. . . Kodi iwe uchita chiani? Amuna ndi abale, kodi ife tichite chiani?

Tsopano pamene iwo anamva izi, iwo analaswa mu mtima mwawo, ndipo anati . . . Amuna ndi abale, . . .

. . . Petro anati kwa iwo, Lapani, ndi kubatizidwa aliyense wa inu mu dzina la Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha tchimo, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.

Pakuti lonjezo liri kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa iwo omwe ali kutali komwe, ngakhale onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawaitana.

Izo zinakhazikitsa icho kwanthawizonse. Palibe munthu konse, mu nthawi iliyonse, akanakhoza konse, konse kusiyanita Zimenezo.

455 Mpingo wa Katolika unabwera motsatira, mmalo moti azimizidwa, iwo amakonkha. Mmalo moti azigwiritsa ntchito Dzina la Yesu, iwo anatenga, “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.” Sizinaphunzitsidwepo konse mu Baibulo.

456 Munthu aliyense, kuchokera pa nthawi imeneyo mpakana, anali kubatizidwa mwa kumizidwa mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo ena anali atamizidwa ndi Yohane Mbatizi, yemwe anamubatiza Yesu, ndipo Paulo anawauza iwo kuti sakanakhoza kulandira Mzimu Woyera monga chomwecho. Iwo ankayenera kuti abwerere ndi kudzabatizidwanso, kachiwiri, mu Dzina la Yesu, iwo asanalandire konse Mzimu Woyera. Ndi angati akudziwa kuti ilo ndi Lemba? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Machitidwe, mutu wa 19. Ndi inu apo.

Chifukwa, Ufumu wa Kumwamba unasindikizidwa kwa njira ina iliyonse, mwa lumbiriro la Yesu Khristu, kuti izo zikanakhala zovomerezeka Kumwamba.

...Lapani, ndi kubatizidwa aliyense wa inu mu dzina la Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha machimo anu, . . . inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.

Chifukwa, lonjezo liri kwa inu, ndi kwa ana anu, . . . kwa iwo omwe ali kutali, ngakhale onse omwe Ambuye Mulungu wathu adzawaitana.

Ameni. Tiyeni ife tipemphere.

⁴⁵⁷ Atate, Mulungu, usikuuno, zaka naintini handiredi ndi chinachake zadutsa, komabe kuwonamtima ndi ubwino wa mtima wa munthu zikulilira panobe Mulungu, monga ana kulirira mkaka wa mmaere a mayi wawo. Ife timakukondani Inu, Ambuye. Ife sitingakhoze kukhala moyo popanda Inu. Monga Davide anati, “Moyo wanga ukuchita ludzu lofuna Inu, monga mbawala pofuna khwawa la madzi.” Iye ayenera kuti akhale nawo Iwo, kapena afa.

⁴⁵⁸ Ndipo, Atate, ife tapesa kudutsa mu Malemba, mmbuyo ndi mtsogolo. Osati kuti tikhale osiyana, koma ife tikuwona maseminare awa, ophunzira amwafioroje awa lero, omwe amalalikira molingana ndi kulamulira kwa anthu, ndipo osati kulamulira kwa Mulungu. Chotero, Ambuye, ife sitiri kuwanyoza anthu amenewo, koma ife tikunyoza zinthu izo zomwe iwo amaphunzitsa. Chotero, Ambuye, ife tikupempha kuti iwo akhale m'bale wathu. Ife tikupempha kuti Inu muwakhululukire iwo pa cholakwitsa chawo. Ndipo ife tikupemphera kuti iwo abwere ku Lemba, kuliwerenga Ilo, osati momwe seminare ina imaphunzitsira Ilo, koma molingana ndi momwe Mulungu analilemba Ilo.

⁴⁵⁹ Ife tikupemphera, Mulungu, tsopano, kuti oyenera awa akubwera usikuuno ku ubatizo wa mmadzi. Pamene m'busa wathu wolimba akuyenda kupita mu guwa ili kuchokera apa, kuti azilalikira Uthenga, Uthenga uwu womwe; ndiyeno mpaka ku dziwe la ubatizo, kuti akawamize. Perekani, Ambuye, kuti aliyense wa awa alandire Mzimu Woyera, chifukwa Inu munapereka lonjezo, Inu mudzalandira Mzimu Woyera.” Mulole Mzimu wa Mulungu ukhale ukuyembekezera pamwamba pa madziwo, kuti uwalandire oyenerawo usikuuno, pakuti ife tikuwapereka iwo mmanja Anu, mu Dzina la Yesu Khristu. Amenii.



BUKHU LA AHEBRI

Mauthenga khumi ndi umodzi awa a M'bale William Marrion Branham, anaperekedwa mu Chingerezi kuyambira Ogasiti 21 kudutsa Seputembala 22, 1957, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org